



ZOYAMBIRA

Gwero ndi Cholinga cha Moyo

**Ndemanga pa
Chiphunziso cha
M'baibulo
Kwamunthu kapena
Gulu.**

**Zolembedwa Ndi
Fred Morris**

**Wotanthauziridwa
ndi Pastor Jones
Chamangwana**



Genesis Gawo 1

Mutu 1 mpakana 11



Kwa Wowelenga kapena Otsogolera

Ndemanga izi ndizothandiza kufotoza Baibulo mosavuta komanso momvetseseka. Zimakhalanso zosavuta kutanthauzira. Mutha kugwirisa ntchito mabukhuwa pophonzira Baibulo panokha komanso mumagulu. Munthu aliyense akhale ndi bukhu lake ndi Baibulo lake ngati ndikotheka.



Kuwelenga Baibulo: Pamene mwaokaona mawu awa, zikutanthauza kuti inu kapensa ntsogolere wagulu ayambe kuwelenga ndime ya m'baibulo musanawelenge bukhu.



Phunzirani izi: Pamene mwaona mawu awa, akuthandizeni kuyang'ana chinthu chachikulu choti muziwe komanso kugawana ndi ena pothandiza kuti aliyense akule mu nzeru M'baibulo komanso kumvetsesa choonadi cha Mulungu.



Lankhulani za izi: Pamene mwaona mawu awa, Pali mafutso ozipempherera ndikuziyankha nokha kapena kukambirana pagulu. Ndiothandizanso owelenga kukumbukira ndime za m'baibulo.



Ganizirani za izi: pamene mwaona mawu awa, funso likufunikira nthawi yocholuka kuti munthu asinkhesinkhe.



Mabokosi ophunzira odulidwa nzele: Pamene mwaona izi, uthengawu ukupereka maphunziro oyenjezera okhuza moyo panthawi imene ndime ya m'baibulo inkalembedwa komanso ndikuthandiza kaphunzidwe kalero.

Kuyamikira: Mawu a m'Baibulo, otengedwa mu HOLY BIBLE New International Reader's Version, ndi ovomerezeka © 1996, 1998 by International Bible Society. Inaperekedwa panthawiyo ndi chilolezo cha Hodder & Stoughton Ltd., membala wa Hodder Headline Group. Maumwini onse ndi otetezedwa. Onani pa intaneti pa: www.biblestudytools.com/nirv

Zithumzi ndi Zokopera © Global Recordings Network (GRN). Kugwiritsa Ntchito Chilolezo.

Genesis Mutu 1 Manna Bible teaching commentary © 2001, 2003, 2006, Fred Morris, Manna Publications (USA) Inc. Maumwini onse ndiotetezedwa.

Mulungu watilola kusindikiza mutu uwu mumayiko osatirawa:

Kope Yosinthidwa muchingerezi chapadziko Lonse Kusindikizidwa ku UK M'chaka cha 2001

Reprinted 2001 in Kenya (English), Mongolia (Mongolian) and Bulgaria (Bulgarian); Reprinted 2002 in Kenya (Swahili) and Rwanda (Kinyarwanda)

Second edition published 2003 in Kenya and Uganda (English); Reprinted 2004 in Kenya (English and Swahili) and Malawi (Chichewa); Reprinted 2005 in Liberia and Ghana (English) and Tanzania (English and Swahili)

Third edition published 2006 in Uganda (English). Reprinted 2007 in Myanmar (English); Reprinted 2008 in Tanzania (English), Togo (French), Ethiopia (Sidama) and D.R. Congo, Katanga (Kiluba and French); Reprinted 2009 in D.R. Congo, Katanga (Kisongye and French), Benin, Burkina Faso and D.R. Congo, Kinshasa (French), Myanmar (Tiddim Chin), Cameroon (English and French), Nigeria (English) and Armenia (Armenian); Reprinted 2010 in Myanmar (Tiddim Chin), Pakistan (Urdu and Saraiki) and Cameroon and Zimbabwe (English); Reprinted 2011 in Egypt (Arabic), UK (English and French), Cameroon (French), Cameroon for Chad (French) and Kosovo (Albanian); Reprinted 2012 in India (Telugu and English), Cameroon (English), Nigeria (English) and Armenia (Eastern Armenian); Reprinted 2013 in Zimbabwe (English), Dem. Rep. Congo, Katanga (Kiluba, Kisongye and French), India (English and Telugu), Pakistan (Saraiki) and Armenia (Eastern Armenian); Reprinted in 2014 in Mozambique (Portuguese), Ethiopia (Amharic), South Africa (English), Cameroon (English and French), Pakistan (Saraiki); Reprinted in 2015 in the Ivory Coast (French), Mozambique (Portuguese), Dem. Rep. Congo, Katanga (French) and Armenia (Eastern Armenian), Malawi (English Braille); Reprinted 2016 in Tanzania (Swahili), Dem. Rep. Congo, Katanga (French); Reprinted 2017 in Ethiopia (Sidama), Malawi (English), Cameroon (French), D.R. Congo, Katanga (French and Swahili); Reprinted 2018 in Zambia (English), Cameroon (French), Tanzania (Swahili); Reprinted 2019 in Malawi for Zimbabwe (English), Myanmar (Burmese), Zambia (English); Reprinted 2020 in Cameroon (English), Zambia (English); Reprinted 2021 in Zambia (English), Nigeria (English), Liberia (English); Reprinted 2022: Mozambique (Portuguese), Malawi (English, Chichewa), Zambia (English), Mexico (Spanish). Reprinted 2023: Zambia (English), Kenya (English), Myanmar (Hakha Chin). Reprinted 2024: Malawi (Chichewa), Zambia (English).

Genesis gawo 1: Mutu 1 to 11

MAWU OYAMBIRIRA

Genesis ndi limozi mwa mabukhu asanu achipangano chakale otchedwa Torah mu Chihebri. Mbiri ya ntchito yolenga ya Mulungu inaperekedwa kwamibado yambiri. Inalembedwa muchiyankhulo cha Chihebri zaka 3500 zapitazo. Mulinso zolembedwa zopatulika za Mulungu mwiniwake, pachiyambi pamagome a miyala, komanso ndi Amose pamagome adongo.


Amatiuza zokhuza:

- Mene Mulungu analengera Dziko ndi chirichonse chirim'menemo.
- Zolinga cha Mulungu ndi cholinga cha moyo.
- Zolinga zabwino ndi zoyipa zomwe.
- Ubwino wa ukwati pakati pa mamuna ndi mkazi.
- Ubwino okhala ndi ana.
- Mmene tchimo umatilekanisira ndi Mulungu.
- Mmene tchimo limaonongera dziko.
- Mmen Mulungu amalangira tchimo.
- Mmene Mulungu amafunira kutipulumusa ku tchimo.

BAIBULO NDI CHIYAMBI CHA MOYO

Genesisi ndi bukhu loyamba la m'baibulo. Limatiwuzza zoonza zake za chilengedwe cha Mulungu, zokhuza zomwe anazilenga ndichifukwa chomwe anazilengera. Chipangano chakale chonse chimatiuza zimene zinachitika Yesu asanabwere, mwana wa Mulungu ndi mpulumutsi amene anabwera kuzakhala padziko lapansi. Ndimbiri yantchito ya Mulungu pa dziko kuyambira kwa Adamu ndi Eva, kenako kwa Noah ndi banja lake mpakana kwa Abraham ndi banja lake. Koma uthenga waukulu m'baibulo ndiwoti tingathe kukhala ndi moyo wosatha kumwamba ndi Mulungu ngati timvera iye komanso tikakhulupirira kuti Yesu Khristu ndi mwana wake komanso mpukuusi. Yesu ndiye amapangisa kuthekere koti ife tikamudziwe Mulungu!

Tingathe kuona zodabwisa za Mulungu muchilengedwe komanso mu mtambo usiku. Kuchuluka kwa zomera, zinyama ndi nyenyezi zimatiuza ife kuti Mulungu alindimphavu zazikulu. Mulungu anazilenga zonsezi ndipo ife sitingazisinthe. Sitingalese Dzuwa kutuluka



kapena mafunde kubwera! Koma tchimo ndi kusamvera kumagwesa ndi kumaononga zomwe iye anazirenga.

Komabe, Mulungu ndiopambana zomwe anazirenga. Amagwira ntchito pazolengedwa zake. Ndimfumu yakumwamba ndi dziko lapansi. Baibulo limati iye ndiye Mbuye wazinthu zonse. Iye ndi Yahwe, Mulungu wankulu, Mulungu wolemekezeka. Iye ndi Mbuye ndi Mfumu chifukwa analenga dzikoo lonse. Chilichonse cha dzikomo ndichake. Choncho pakuti Mulungu anandilenga, iye ndiye Mbuye wanga.

Timaziwanso kuchokera m'baibulo kuti Mulungu ndi munthu. Amalingalira, amarenga, ndipo amafuna ife tizimukonda.

M'baibulo, Mulungu amatiuza ife zokhuza iye mwini. Tingathe kumuziwa mmene timaziwira munthu aliyense. Mulungu alindinjira zodabwisa zomwe angatiwoneseremene aliri. Choyambirira anationesa kale ukulu wake kuzera muzinthu zomwe anazirenga. Kenako, anatomiza mwana wake Yesu Khristu kudziko lapansi kwa zaka 33. Akhristu amakhulupirira kuti Yesu sopano ali kwa Mulungu ndipo azabweranso kudziko lapansi siku lina posachedwapa. Alikumwambandi atate ake. Timakhulupiriranso kuti Yesu anali ndi Mulungu kumwamba asanabadwe mwa Maria kudziko lino lapanzi kuzera mwa mzimu woyela wa Mulungu. Yesu adawuza atsogoleri a Ayuda nthawi imeneyi "NDIINE ngakhale Abraham asanabadwe" (Yohane 8:58). Yesu adagwiritsa ntchito mawu opatulika omwe Mulungu amagwiritsa ntchito "NDIINE" (Eksodo 3:14). Yesu anabwera kuzakhala pa dziko kuti ationese Mulungu. Anabwera kuzationesa mmene Mulungu alili. Iye alingati Mulungu chifukwa ndi mwana wa Mulungu komanso Mpulumusi wa Ayuda olonjezedwa ndiwa akhrist kwinakulikonse.

Timakhulupirira kuti Yesu anali ndi Mulungu Atate ngakhalenso dziko lisanalengedwe. (Genesis 1:26; Yohane 1:3; Akolose 1:16; Ahebri 1:2).

Baibulo limati Yesu Khristu amalumikizisa zinthu zonse. kutanthauza kuti iye ndiye olamulira. Palibe chingachitike popanda iye. Amachita chilichonse munjira yokodweretsa Mulungu. Amalola kuti zinthu zichitike, zimene ndimbali zakukonzakwake kuti akabwezere anthu kwa Mulungu Atate wake ndikukamutamanda. Amatumizanso mzimu wake woyera kudziko lapansi kuti ukaphunzitse anthu choonadi cha iye mwimi. Mulungu ndi "Mtatu mu mmodzi". mzimu woyera umatithandiza kudziwa Yesu ngati Mbuye ndi Mpulumutsi wathu. Amatithandiza kudziwa Mulungu ngati Atate wathu. Amatithandizanso kudziwa Mzimu woywra.

KODI MULUGU ALI NGATI NDANI?

Sono kodi Mulungu ndimunthu otani? Mulungu ndi Mzimu komanso Mulungu ndi munthu. Mulungu amakonda ndikusamala. Sachita cholakwika komanso sakondwera ndi zolakwika zomwe anthu amachita. Zolakwika zimenezi zimatchedwa Tchimo. Zimawachita chifukwa timaziwa chabwino ndichoyipa koma timasankha kuchita zoyipa. Sakondwera pamene anthu akumwalira asanamve ndikuphunzira za iye mwini. Sakondweranso pamene ana akumwalira asanabadwe kapena atangobadwa kumene. Amafuna anthu aphunzire za iye mwini choncho iye

azakhala mwaife muuzimu. Munjira imeneyi, tizaona chikondi ndichifundo cha Mulungu monga momwe khristu anaonesera zaka 2000 zapitazo padziko pano.

Isadayambike nthawi, Mulungu anali ndi maligaliro olenga dziko. Zimene zikutanthauza kuti adatiziwa ife ndimayina anthu ngakhale tisanabadwe! Amaziwa ngakhale kuchuluka kwa tsitsi m'mutu mwathu. Mulungu ndiwa Mkulu, amaziwa chilichonse. Amaziwa zomwe zichitike Mawa komanso amaziwa yemwe ati azabadwe chaka chamawa. Malingaliro athu sangamvetse ukulu ndidabwisa kwa Mulungu. Amadziwa chilichonse chomwe chinalipo, chilipo ndichomwe chizakhalepo.

Mtumiki wa Mulungu adalemba Kalero, "Yehova, inu ndinu Mulungu wanga. Mwachita zodabwitsa. Munazikonzeratu kalero" (Yesaya 25:1). Tonse ndife gawo yazolengedwa zake zodabwitsa. Mulungu sakondwera pamene tchimo likuononga dziko lomwe analirenga. Tiwerengabe kuti Mulungu amatilola kusankha pakati pazabwino ndi zoyipa. Ndife omasuka Kusankha, Tingathe kukonda Mulungu kapena kusankha tchimo. Amationetsa mmene tingakhalire ndi chikhulupiriro mwa iye ndikutalika komvera iye ndikumupephedza.



Lankhulani za Izi:

1. Ndinu okonzeka kuwelenga bukhu la Genesis ndi malingalilo Omasuka?
2. Mukufunitsisa kupeleka nthawi yanu pakumvetseza za chiyambi ndi cholinga cha moyo zili mu Genesis?
3. Mungakwanitse kukana chiphunzitso chonama chomwe munamva kuchokera kwa omwe sadziwa ndikukonda Mulungu?



Ganizirani Izi: Pempherani kuti Mzimu ukulankhuleni pamene kukuphunzira Malembo Woyela a Mulungu M'baibulo. Dziwani kuti Yesu Khristu, mwana wa Mulungu, ali ndi Atate kumwanda, kusaka chipulumutso chanu sopano kuzela mukudzuzika kawake pantanda chifukwa chamachimo awanthu nza 2000 zapitazo.

Sopano tiyeni Tiyambire Pamayambiriro...



Kuwelenga Baibulo: Genesisi Mutu 1



Phunzirani Izi: *Chidachitika ndi chiyani Mulungu atalenga Dziko ndikugawa madzi, ena pamwamba pa thambo ndi ena panso pa thambo. (ndime 1-10); Mulungu adayankhula mawu polenga udzu ndi zomera ndi Mitengo kuti ibale zipatso ndinso dzuwa, mwezi ndi nyenyezi kuti zilamulire dziko usana ndi usiku. (ndime 11-19); Analenga Nsomba, Mbalame, ndi zinyama (ndime 20-25); anaLenga munthu muchifanizilo chake ndikumpasa zomera kuti azidya (ndime 26-31).*

NTCHITO YA MULUNGU YOLENGA

Genesis ali kumayambiriro kwa Baibulo. Amatiuza zokhuza chiyambi chachirichonse ndicha moyonso. Amatiuza xokhuza chiyambi chi cholinga cha moyo. Genesisi amati "pachiyambi Mulungu analenga Kumwamba ndi Dziko

lapansi” (Genesis 1:1). (Mawu oti “Mulungu” muchi Hebri chenicheni amathanthauza Mulungu Atate, Mulungu Mwana ndi Mulungu Mzimu Woyera).

Pachiyambi, dziko linali losaumbika (1:2). Lopanda Anrhu, lopanda mamawa kapena usiku, Dzuwa osatuluka kapena kulowa, popanda masiku, masabata ndimiye. Linali lopanda kanthu ndipo Mzimu waMulungu ‘umayendayenda pamwamba pa madzi’. Kenako Mulungu analenganitsa mtunda ndi madzi. Anayika nthawi ndimalo ndi nyenye (dzuwa) ndi dziko. Padziko lapansi, Mulungu analenga masiku, masabata, ndi usiku ndi mamawa. Mulungu analenga zomera ndi mitengo, analenga nyama ndi ziweto. Kenako analenga Adamu, munthu oyamba padziko lapansi.

‘Kurenga’ ndi mawu apaderadera muchi Hebri. Ndi mawu a Mulungu yekha ndi ndi ntchito yake. Ndi Mulungu wamoyo yekhayo angale kumwamba ndi dziko lapansi kuchokera popanda kanthu. Anthu amapanga zinthu kuchokera kuzomwe Mulungu anazilenga kale.

Mawu oti ‘Kurenga’ adagwiritsidwa ntchito katatu mugawoi yoyamba ya Genesisi. Mundime 1, Mulungu analenga dziko lapansi ndi zomwe timazona kumbamba zotizungulira ife: zimene zikutanthauza ‘chirichonse’. Mundime 21, Mulungu analenga zinyama. Mundime 27, Mulungu analenga Munthu.



MULUNGU WAMPHAVU ZONSE: Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera

Akhristu amakhulupirira kuti Mulungu ali patatu: Atate (chihebri ‘Yahweh’), Mwana (Yesu, chihebri ‘Yeshua’) ndi Mzimu Woyera, atatu m’modzi. Nthawi zina ife timati uyu ndi Mulungu **MUUTATU WOYERA**. Izi zimatanthauza kuti Yesu ndi Mzimu Woyera waMulungu anali limozi ndi Mulungu Atate pachiyambi, ngati Mulungu m’modzi, dziko lisanapangidwe. Ndikuona Baibulo limati;

- “Tiyeni tipange munthu muchifaniziri chathu” (Genesis 1:26).
- “Munthu wakhala ngati mmodzi wa ife” (Genesis 3:22).
- Kenako mbaibulo, mawu oti IFE anagwiritsidwa ntchiti:
- “Bwerani Tiyeni IFE titsike ndikukasokoneza chilankhulo chawo” (Genesis 11:7).
- “Ndidzatuma yani, ndindani amene azatipitira IFE?” (Isaiah 6:8).

Ichi ndichifukwa chake Yesu anati, “Timanena zomwe Tikudziwa ndipo Timaperekera umboni wa zomwe Tazona” (John 3:11). Yesu amasimikizira kuti analiko nkale lomwe Abraham asanakhalepo (John 8:58).

MASIKU ASANU NDI LIMODZI WOLENGA

Patapita nthawi dziko lidakali losaumbika, Mulungu adalankhula kasanu ndi kamodzi polenga dzuwa, Mwedzi, dziko lapansi ndizamoyo zake zonse. Mulungu analankhula kasanu ndi kamodzi kuti chilichonse anachilenga chinali chabwino (Genesis 1:9, 12, 18, 21, 25, 31). Timaziwona zimenezi m’dziko lotizungulirali, kupatulapo zoyipitsa zoyambisidwa ndi munthu.

Mulungu adatipasa zolemba zake pa Torah zomwe zimatiuza mmene anarengera dziko lapansi ndi zonse zokhalamo. Izi zidalembedwa mu Genesisi mutu 1 ndipo zidachitika zaka 8000 zapitazo, choncho kuti mungaziwerengere nokha. Tikuyenera kuthokoza Mulungu chifukwa cha Baibulo lomwe limatiuza zomwe zidachitika 'pachiyambi' ndi kenako Adamu, Nowah ndi Abraham pambuyo pa Yesu Khristu kutsikira kudziko lapansi m'dzika 2000 zapitazo. Tikadakhala opanda Baibulo, sitikadaziwa komwe dziko lodabwisali linachokera. Olo chifukwa chani timakhala muno m'dziko. Mubaibulo, Mulungu amatiuza zonse zachiyambi ndi cholinga chamoyo, kuti timumvere ndikumu pembeza iye ndi njira yake yachipulumutso, yamphatso yamoyo woyera wosatha.

Zatsopano zikuvumbulutsidwa nthawi zonse zokhuza zodabwitsa za dziko. Mulungu sanatiwuze zonse zammene anarengera dziko, koma anatiwuzwa zonse timayenera kudziwa mumawu osavuta. Ziri mu Baibulo. Chirengedwe chinachitika chifukwa Mulungu anachifuna. Adayankhula mawu pochilenga ndiponso adati zidalibwino. Adakonda zomwe adazipanga ndiponso amalandira mapemphero ndi matamando athu.

MAWU A MULUNGU WOLENGA

Mawu a Mulungu ndi a mphamvu ndi opasa moyo. Mulungu adati, "kuwale" ndipo kunawala (1:3). Sikukadakhala moyo pa dziko kupanda kuwala ndi kutentha ndipo cholinga cha Mulungu kunali kulenga moyo. Izi kuphatikizira munthu muchifaniziro chake. (1:27).

Pmene Mulungu amasiyanisa kuwala ndi m'dima. Adautchula kuwala 'usana' ndipo mdima adautchula 'usiku'. Kuwalako kumapeleka kutentha. Kuwala kutawoneka, Mulungu anati zilibwino. Chilichoncho chomwe Mulungu adachipanga chinalibwino. Kenako Mulungu anakankha madzi ndikupanga mtunda (v.9). madzi ena anali pansu pa thambo ndipo ena pamwamba pa thambo. (6-7). Koma panthawiyo sikudagwe mvula. Palibe madzi omwe amagwa kumwamba koma padali madzi ambiri pansu. Nkhungu inkapangisa nthaka ya dziko kukhala yonyowa (2:5, 6).

Ndipo Mulungu anati, "Madzi azazigwe ndizinthu zamoyo ndipo mbalame ziwuluke mulenglenga" (1:20). Izi zidachitika kwakanthawi kochepe. Cholengedwa chilichonse chinazazidwa ndi mbewu mkati mwake yamibado yatsopano. Mulungu adalankhula ndipo kudakhala nsomba Nyanja ndizokunya zake mmenemo. Mulungu sadali okondwa kupanga mtundu umodzi kapena iwiri yokha. Adapanga mazana mazana a mitundu yotsiyanatsiyana ya nsomba ndi mbalame.

Mulungu adaphimba nthaka ndimitundu yochokuka ya udzu ndi zomera za nthanga zakezake. Kenako Mulungu analenga nyama ndi nyerere kuti zikadye zomera. Mulungu analenga mitundu yochulukuka ya nyama, zadzimuna ndi zadzikazi, zakukhomo ndizakutchire, Anyani ndi zinyama zina zomwe zinatha padakali pano. Padalinso zinyama zambiri zowuluka ndizokwawa, zilizonse ndi madzira ake.

Mtundu uliwonse umabeleka ana amtundu wakewake kuti zizipanga mtundu ofana wa nsomba, mbalame, nyerere kapena zinyama. Mulungu adawonetsesa kuti mtundu uliwonse uzibala ntundu ofanana nawo pa chaka, chaka ndi chaka.

Anagwiritsa ntchito DNA kuchokera m'bukhu lake la moyo polenga mtundu uliwonse.



Mulungu Analenga Zamoyo Zonse

Mulungu anali okondwera ndikumwamba ndi dziko lapansi lomwe iye anazilenga. Zidali mmene iye anaziligalira ndi kuzikonza kuti zikhalire. Iye anaona kuti chilengedwe chake chinali bwino. Ndipo anati, "nthaka imere udzu tchire ndi mitengo ya zipatso ndi nthanga zake momwemo". Eya, analenga zomera zoyambirira ndinthanga zake kale mwaizo. Adayika moyo mukanthanga kalikonse. Ndi Mulungu yekha angapeleke moyo. Nthanga iliyonse idapangidwa mkati mwake kuzabala zomera zofanana nazo. Munjira iyi, Mulungu adawonetsesa kuti mtundu uliwonse wazomera uzibala ntundu ofanana nawo pa chaka, chaka ndi chaka, popanda kusintha.

Nthanga iliyonse yomwe anthu amayisiya malo owuma kwa zaka mazana mazana izakula ndikukhala yamtundu omwewo. Akaswiri asayansi amatiuza kuti bewu iliyonse ili ndi "mawu ake amoyo" mwayo otchedwa DNA. Munjira iyi Mulungu anapereka "mawu ake amoyo" mwa zomera zonse ndi zinyama zonse. Aliwjonse ndiwosiyana. Mtundu uliwonse uli ndi DNA yake. Mawu a DNA onenedwa ndi Mulungu amalamulira kakulidwe kake. Palibe chimaloledwa kukula mumtundu wina. (Munthu amayesela kusintha zomwe Mulungu anazipanga, ndi 'mankhwala', ndi 'Kusankha', ndi 'kuswanisa' ndiponso kusintha maselo kapena DNA). Mulungu adayankhula olenga ndipo chomera chilichonse ndinyama chilichonse chinajpangidwa. Ndipo chilichonse chinalibwino.



Moyo ndiwamtengo wapatali chifukwa Mulungu anawulenga. Zonse zamoyo anazilenga ndiye. Anapeleka moyo wina kumitengo ndizomera, Moyo wina munsomba, komanso moyo wina muzinyama ndi nyerere.

Nyama ndi anthu zikuyenera kukhala ndi mpweya kuti zizipuma, choncho Mulungu analenga zomera koyambirira kuti zipeleke mpweya omwe timafuna. Tikuyenela kusamalira zomera ndi mitengo, zimatipasa chakudya ndi mpweya wabwino.

Mulungu analenga dzuwa kuti lipereke maola akuwala. Analolanso m'dima koma mwakanthawi kenakake kokha. Usiku odzidzira umapanga nkhungu (chifunga) ndi mame kuti athirire zomera pamene zikupanga mpweya oti zinyama zizipuma.

Dzuwa lathu zimapereka kuwala ndi kutentha kudziko. Zomera zimagwiritsa ntchito zomera ndi kutentha kuti zikule. Dzuwa limasunga dziko kukhala lofunda, choncho kuti titsadzidzidwe ndikufa. Anapanganso nyenyedzi ndikuziyika m'malo mwake. Zimakhala munjira yomwe Mulungu anazipasa nthawi zonse. Iyi ndi gawo lina la dongosolo lomwe Mulungu analiyika muchilengedwe chake.

Potsirizira pake zolengedwa za Mulungu zinali m'malo. Dziko, Nyanja, mitengo, zipatso, zomera, nyerere, mbalame, nsomba ndi zinyama zomwe iye anazilenga. Kenako Mulungu analenga munthu oyamba "muchifaniziro chake", Chimene chinali cholinga chachikulu chachilengedwe cha Mulungu.

CHIFUKWA CHIYANU MULUNGU ANALENGA MUNTHU

Pasiku lachisanu, Mulungu anamaliza kulenga zinthu zozizwitsa zonsezi, koma 'panalibepo munthu oti azigwira ntchito' (2:5). tikudziwa kuti Mulungu analenga munthu kuti azitsamalira chilengedwe chake (1:28). Choncho tikuyenera kumvera Mulungu ndikutsamalira dziko lomwe analilenga. Kunali kwabata, kopanda namodwe ndizoyipitsa. Zamoyo zonse zimkakula bwino ndikukhala kwanthawi yayitali.

Genesis 1 amatiwuzza chomwe Mulungu analengera munthu:

- Kuti akhale ngati Iye 'muchifaniziro chake' (1:26, 27).
- Kuti alamulire ndikusamalira chilengedwe chake (1:26).
- Kuti akakhale ndi ana ndikuzadza dziko lapansi (1:28).

Mulungu amasamalira munthu ndizinyama zomwe anazilenga kuzera mukudya zinthu zabwino zomwe zimamera padziko (v.29) cholinga chake chinali choti tilandire chikondi chake ndikuti ifenso timulambire Iye.



Lankhulani za izi:

1. Ndichani chimene Mulungu anazilengera chomusanalatsa iye?
2. Ndichani chimene Mulungu anamulenga chosangalatsa munthu?



Kuwerenga Baibulo: Genesis mutu 2



Phunzirani za izi: *mdalitso wa tsuku la chitsanu ndichiwiri ngati siku Lopatulika (ndime 1-3); uthenga onse wadziko ndi wamunthu oyamba ndi wamunda waedeni ndi mitsinje yake (v.4-14); Mulungu anamuuzza Adamu kuti atchule mayina mbalame ndi zinyama (v.15-20); Analenga mkazi kuchokera kunthiti ya Adamu ngati omuthandizira wake ndipo anali amaliseche ndiopanda manyazi (v, 21-25).*

MMENE MULUNGU ANALENGERA MUNTHU

Genesis 2 amatiuzza mmene Mulungu analengera munthu. 'Mulungu Atate anaomba munthu. Anamupanga kuchokera ku fumbi lamunthaka. Anauzira mpweya mwa iye, mpweya wamoyo ndipo munthu adakhala wamoyo' (2:7).

Mulungu anagwiritsa ntchito zinthu zochokera ku nthaka pomwe amalenga moyo (2:7, 19). Ngakhale anthu (ndizinyama zina) saoneka ngati fumbi ndidothi ndi miyala, tinapangidwabe kuchokera kuzinthu zofanana za nitrogen, oxygen, carbon, hydrogen, calcium ndizina zotero. Tinapangidwa kuchokera kuzinthu zofanana zomwe Mulungu anagwiritsa ntchito pachiyambi popanga zomera ndi zinyama zina.



Chisinthiko kapena Chilengedwe?

Baibulo limati munthu ndi mkazi anali chilengedwe chapaderadera cha Mulungu. Anali ngati Mulengi wawo ndipo anali osiyana ndi ziweto ndi zinyama zinazonse zapadziko.

Ambiri amakhulupirira kuti anthu anachokera ku anyani, koma izi sizoonza kutengera ndi Baibulo kapena kutenge mafupa akalekalero omwe timapeza munthaka. Charles Darwin amakhulupirira kuti kusintha kwakung'ono kwazinthu zamoyo kapena zomera kumatulusa zamoyo zapamwamba. Ichi chimatchedwa chiphunziso cha chisinthiko. Chonchobe akaswiri azasayansi adasimikiza kuti ndizosatheka nyama kukhala munthu. Palibe kulumikizana kulikonse pakati pa mitundu yazinyama kapena zomera zomwe zidapezeka zikusimikizira chiphunzitsa ichi. Kusowa kwa kusowekera kulumikizana kwa Darwin kudakasowabe.

Akhristu amakhulupirira kuti galu adali galu, nyani adali nyani, munthu adali munthu. Sizinayambe zalumikizidwapo. Mitundu yonse ya agalu ndi agalu. Mitundu yonse ya anyani ndi anyani. Mitundu yonse ya anthu ndi anthu. Mulungu anawonetsesa kuti mtundu uluwonse wazinyama kapena zomera zisasinthe kupita ku mtundu wina. Nthanga kapena madzira ake amakhala mtundu omwewo nthawi zonse, koma ndimitundu yambiri yosiyanasiyana. Nthanga ndi madzira ake analengedwa mkati mwake ndi Mulungu panthawi yoyamba pomwe anakalenga zomera ndi zinyama.

Kaswiri wa sayansi Charles Darwin sankadziwa za izi zaka 150 zapitazo koma lero akaswiri asayansi adasimikiza kuti palibe mbali yachinyama kapena chomera chimalola kusintha kukhala chinyama kapena chomera china. Mawu a DNA amaonetsesa kuti apange mbewu ya ichocho chokacho basi (onani Genesis 1:12). Mulungu adayankhula mawu, choncho chilichonse chinalengedwa ndipo pamapeto pake anapanga munthu 'muchisanizilo chake'.

Matupi athui anapangidwa muchisaniziro cha Mulungu atate, muulemerero ndi cholinga chake, osati kukwaniritsira zokhumba za ife tokha. Ngati mumakhulupirira chilengedwe cha Mulungu, ndekuti muli ndicholinga chapaderadera m'moyo, cholinga chokhalira ndi moyo, ndi chiyembekezo cha moyo winawo kuzera mukumvera ndi kukhulupirira Mulungu. Izi ndizotheka pano kuzera mukukhulupirira Mwana wa Mulungu, Yesu Khristu, yemwe anachoka kumwamba kwa Atate ake kuzazuzika pamtanda chifukwa chamachimo athu asanabwererenso kumwamba.

Choncho, Adamu, Munthu oyamba, anapasidwa moyo osatha wa mzimu ngati wa mzimu wa Mulungu. Anali ndi nzeru ndipo amatha kuganizira za zinthu. Ankaziwa Mulungu ngati mzake. Mulungu anali ndiubale wapafupi ndi Adamu.

Zinyama sizingayankhule ndi Mulungu kapena kudziwa Mulungu mmene munthu angacjitire. Mulungu anafuna munthu oti azimukonda, munthu ngati iye mwini, choncho anapanga Adamu 'mwachifaniziro chake'.

Mulungu anamulenga Adamu wankulu kale, Sadakhalepo mwana. Adamu amalankhula ndi Mulungu ndikumva zomwe amanena. Sankapanga phokoso ngati nkumba kapena anyani. Ankanena mawu achilankulo chomveka bwino, ndipo ankamvetsetsa zomwe Mulungu ankamuuzira. Ankadziwa chabwino ndiponso

ankasankha kuchita chabwino. Zinyama zinalibe mzimu wa nzeru ngati munthu. Munthu salingati chirichonse chomwe Mulungu anachilenga. Salingati zinyama, nsomba, mbalame kapena mitengo. Munthu angathe kuganiza ngati Mulungu. Munthu angathe kuziwa chabwino ndikusankha kuchichita. Timati munthu ndiwa 'umunthu'. Munthu angathe kumuziwa Mulungu komanso kumayankhula mawu owonadi a Mulungu.

Kenako Mulungu anamuwuzwa Adamu kuti apase mayina zinyama. Zinyama zinabwera kwa Adamu ndipo anapereka mayina kwa zonse (2:19). Iyi ndi nthawi yoyamba imene Mulungu anampasa ntchito munthu kuti agwire kugwiritsa ntchito mawu kuti alankhule. Adamu anaziwa malingaliro a Mulungu ndipo analankhula mawu ake.

MALO APADERA A ADAMU

Mulungu ndiwokonda ndiwa nzeru. Pamene Mulungu anapanga Adamu, anamutengera kumunda wapadera (2:8). Mulungu anapanga mundawo mu Edeni. Malo ake enieni anaperekedwa m'baibulo (2:10-14). Mulungu anayika chabwino chilichonse m'mundamo kuti Adamu akasangalale. Chilichonse chomwe Adamu amachifuna chinali mom'mo.

Mulungu anamuuzwa Adamu kuti azikhala m'mundawo ndikuti aziusamalira. Anamuuzwa Adamu mmene angasamalire zomera ndi zinyama. Cholinga cha Mulungu chinali choti munthu alamulire chilengedwe chake. Ndipo kumayenera kumakhala chakudya chokwanira nthawi zonse. Munalinso 'ntengo wamoyo' umenenso ndi ntengo umene uzakule mu dziko lasopanso ukazatha moyo uno (Gen 2:9; Chivumbulutso 22:2). Ndipo munalinso 'ntengo wodziwitsa chabwino ndi choyipa' (2:9)

Chifukwa Mulungu anati 'Lamulira chilengedwe' (Gen. 1:26), munthu ndiolamulira chilengedwe, ndipo amafuna ntchito. Munthu sakondwera akakhala opanda ntchito! Mulungu anaudza Adamu zoyenera kuchita ndizoti asachite. Anamuuzwa mmene angalamulire moyenera ndi mosamala. Chilichonse chomwe Mulungu amatiuza chichofunika kwa ife. Mulungu ndi Chikondi ndiponso Mulungu ndiwoyenera ndi olondora.

Adamu anali ndi chisankho ndipo anasankha kumvera Mulungu pachiyambi. Adamu amasamalira munda wa Mulungu ndipo Mulungu amamuudza chilichonse. Adamu anali otanganidwa pa siku la chitsanu ndichimodzi kupereka mayina azinyama atakhala ndi Mulungu (2:19). Koma panalibe zinyama zooneka mofanana kwa Adamu.

M'DZAKE WA ADAMU

Zinyama zonse zitadutsa, Mulungu anamuyang'ana Adamu, Atakhala pamenepo yekhayekha. Mulungu anati, "sikoyenera kuti munthu akhale yekha. Ndipanga omuthandizira amene ndiwoyenera kwa iye" (2:18).

Mulungu anadziwa Adamu kuti akufunikira munthu wangati iye, munthu amene amene akhale mdzake. Chocncho anapanga Eva. Pamene Adamu anagona, Mulungu anatenga nthiti waiye ndikupanga munthu wamkazi (2:21-22).

'Muchifaniziro chake... mamuna ndi mkazi, Mulungu anawalenga' (1:27). Eva, nayenso, anapangidwa 'muchifaniziro cha Mulungu'.

Adamu atadzuka, Mulungu anamubweretsera Eva kwa iye. Anawona mwakamozi kuti amawoneka ngati iye. Sanali ngati zinyama, anakhala m'dzake wapadera. Kenako Adamu anamupasa dzinanso. Anamutchula mkzaiyo 'Eva' ndipo anagawana naye chilichonse anapanga. Eva anakhala mkazi wake wa Adamu.

Dziwani kuti:

1. Adamu ndi Eva anali anthu awiri okhawo omwe analowa m'dzikoli mosachiti kubadwa. Anali chilengedwe cha Mulungu chapaderadera.
2. Adamu ndi Eva anali anthu okhawo omwe analowa m'dzikoli opanda tchimo, kupatula Yesu amene nthawi zina amatchedwa 'Adamu wachiwiri'.

TSIKU LOPUMA

Patsuku lachisanu ndichimodzi, Mulungu analeka kulenga (2:1, 2). Mulungu sanalengenso kanthu atangolenga Eva. Mulungu anatchula siku losatiraro 'siku loyera' kapena 'Sabata'. Uku kunali kukhazikitsa nthawi yopuma ya Mulungu, kusangalala kusangalalira zomwe ine anazilenga. Mwapaderadera anasangalala pokhala chiyanjano limozi ndi Adamu ndi Eva. Ichi ndichifukwa chake zipembezo zambiri padziko pano zimasunga siku lasabata lopuma ndi kupembedza Mulungu.

Siku lachisanu ndichiwiri lidali nthawi yosangalala ndi kupuma kwa Mulungu. Dziwani kuti siku lachisanu ndichiwiri linalibe mathero monga masiku ena asanu ndilimodzi aja. Mulungu adakasangalalirabe chilengedwe chake. Choncho ifenso! Njira yabwino yosungira Sabata ndi kupembedza Mulungu, kusangala ndi chilengedwe chake ndiponso kumupasa nthawi Mulungu kuti akachedze nafe. Tikuyeneranso kuyetsa izi nthawi dzina pamodzi ndi okhulupirira ena.

Mulungu anayika Mzimu wake omwe mwa Adamu ndi Eva. Anawapasa moyo umene ukuyenera kupitirira mpakanampakana. Zamoyo zonse zinachokera kwa Mulungu, tsono munthu akuyenera kumumvera ndi kumupembedza iye yekha (Eksodo 20:3) choncho timadziwa kuti tchimo limachotsa mzimu wa Mulungu ndi kutiletsa kukhala ndi moyo osatha. Tchimo limazetsa imfa yamuyaya.

Mulungu anakonza kuti siku lina Yesu adzabwere panso pano kuchoka kumwamba ndikuzakhala njira yokhayo tingabwerere kwa Mulungu kuti tikapezenso moyo osatha.



Lankhulani za izi:

1. Kodi Mulungu anatipo chani za siku lachisanu ndichiwiri lasabata (2:2)?
2. Mulungu anamuudza chani Adamu zoti achite, adye ndi kulankhu (2:15, 16, 19)?
3. Mukumvetsapo chani paudio wa Mulungu kwa amuna ndi akazi akumayambiriro (1:26; 2:18, 27)?
4. Mukuziwapo chani pazamitengo yopatuluka iwiri ya munda wa Edeni (2:9, 16, 17)?
5. Kodi njira ya Mulungu pamaukwati ndi mabanja ndiyotani (2:24)?



Ganizani za izi: mukumupempha Mulungu kujiti akuthandizeni kumvetsesa za moyo osatha ndi nzeru yachabwino ndichoyipa (2:9)?



Kuwerenga Baibulo: Genesis Mutu 3



Phunzirani za izi: *Njoka (Dyerekezi) ananyenga Eva ndikupangitsa kuti Adamu ndi Eva achimwe ndipo anali ndi manyazi (v. 1-13); Mulungu atemberera njoka komanso kupenekera kugonjesedwa kwake ndi zizukulu za Eva (v. 14-15); Mulungu alanganso Adamu ndi Eva (v. 6-19) komanso kuwapaa zosowa zawo asanawathamangise mmunda wa Edeni (v. 20-24).*

MULUNGU AMPASA ADAMU LAMULO

Siku lirilonse Mulungu amayenda ndi kukayankhula ndi Adamu ndi Eva. Amafuna kuti iwo amudziwe ndi kumukonda monga ngati dzawo wokondedwa.

Mulungu anati kwa Adamu, “ungather kudya chipatso chantemgo uliwonse m’mundamu, koma usazadye chipatso cha ntengo wodziwitsa chabwino ndi choyipa. Pasiku lomwe uzadyero uzafa ndithu” (Gen. 2:16-17).

Adamu anamvetsetsa lamulo la Mulungu; anadziwa kuti mawu a Mulungu anali owona. Mulungu anamukonda Adamu ndipo amamufunira zabwino. Amadziwa



Kulengedwa kwadziko

Pachiyambi kunali m’cina, madzi ndi Mzimu wa Mulungu.

Baibulo limagwirizana ndi zomwe akaswiri asayansi amati dzinachitika:

- Choyambirira kunali kuwala (komanso kutentha).
- Kenako madzi pansu ndi madzi pamwamba ndimpweya pakati pake.
- Kenako Nyanja, mtunda ndi zomera.
- Kenako dzuwa, mwedzi ndi nyenyedzi.
- Kenako nsomba ndi mbalame.
- Kenako zinyama ndi zinthu zina zamoyo.
- Kenako mamuna ndi mkazi.

Dziko linali losiyana chisanafike chigumula cha nowah (Genesis 7) ndi mmene liriri pano:

- Madzi ankasungidwa mulengalenga apamwamba padziko (Genesis 1:7).
- Mvula sinkagwera nthawi (Genesis 2:6). Nkhungu ndi mame amapereka madzi.
- Znthu amakhala kwanthawi yayitali (Gen, 5:5-32). Kunalibeko nyengo zosiyanasiyana.
- Kunkakhala anthu ena akuluakulu azimphavu (Gen. 6:4) ndi zilombo zikuluzikulu.
- Kunalibe Utawaledza chifukwa sikumakhala mvula kapena namondwe (Gen. 9:13).
- Sikunkakhala kuotcha kapena kudzidzira. Zomera zimamera paliponse. Kunalibeko chipululu.

chomwe chinali chabwino kwamunthu. Anafuna kuti atetedze Adamu ndi Eva kuzoopsa. Amafuna amutetedze Adamu kukusadziwa choipa. Adamu akanamvera kukanakhala kosavuta kugwiritsa ntchito mundawo. Koma Mulungu anamulenga Adamu ndichitsankho. Adamu akanatha kumvera Mulungu kapena kusamumvera. Kusamvera Mulungu ndikolakwika; nditchimo. Tchimo limayenera kulangidwa.

KUTSANKHA PAKATI PA CHABWINO NDI CHOYIPA

Dyerekedzi anafuna kuipisa chilengedwe cha Mulungu. Anabwera m'mundamo kuzayang'ana Adamu ndi Eva. Anagwiritsa ntchito njoka m'mundamo kulankhula ndi Eva. Njoka jitha kukhala kuti inali yokongola. Koma inkatha kunamiza anzake kuposa nyama iriyonse yomwe Mulungu anayilenga (Gen. 3:1).

Dyerekedzi (wankulu wa oyipayo) anali m'ngelo okongola, koma anali wansanje ndiofuna kukhala wankulu kujposa Mulungu. Choncho Mulungu anamuthamangitsa Dyerekedzi kumwamba. (Luka 10:18). Yesu anali ndi Atate ake, Mulungu kumayambiriro (Yohane 17:5). Yesu anaona Dyerekedzi akugwa kuchokera kumwamba.

Eva anamva mawu asatana akumulankhula, ananena zinthu zokhuza Mulungu zomwe sizoon. Satana anafuna kuti Eva asankhe njira yolakwika, kenako kuti apeze mphamvu pamunthu ndijmkazi wake. Satana anafuna kuti akhale mfumu ya zolengedwa za Mulungu.

Mulungu sanganame (Ahebri 6:18). Chilichonse Mulungu amanena ndichoona. Zabozza zonse zimacholera ka Dyerekedzi. Baibulo limati, "mzimu oyipa... chiwanda ... ndiwonama, ndipo mabozza onse amachokera kwiye" (Yohane 8:44).

Satana anamufutsa Eva, "ndizoon kuti ulungu anati musadye chipatso chantengo uliwonse mmundamu"? Satana anasintha mawu amujlungu kufuna kumuonesa Mulungu kukhala wabodza.

Eva anamuuzza Satana kuti Mulungu anati, "mujjsakhuze kapena kudya chipatso chantengo wapakati wamundawu. Mukazatero mjuzafa" (Gen. 3:3).

Kodi Eva anakhulupirira zomwe Mulungu ananena? Kodi anakhulupirira zomwe Satana ananena? Amayenera kusankha pakati pa lamulo la Mulungu ndi bodza la Satana. Anapasigwa mwayi osankha pakati pomvera Mulungu kapena Satana. Ifenso, timayenera kusankha pakati pazabwino ndi zoyipa!

Ena mwa angelo anasatira Satana. Mizimu ya angelo onse omwe sanamvere Mulungu anathamangidwa kumwamba. Iripo yambiri midzimu yoyipayi masiku ano, ndi Satana ngati ntsogoleri wawo. M'baibulo amatchedwa kuti ziwanda. Satana amagwiritsa ntchito midzimu yaziwanda poyesera kupeza mphamvu pamwamba pa anthu. Monga ngati Satana, onse ndiyonama ndipo amayesera kutisocheretsa ndikuti azitiramulira.

TCHIMO LOYAMBA

Satana anaona kuti Eva sanali otsimikizika. Chikhulupiriro chake kaw Mulungu chinali chopanda mphavu, choncho Satana anatenga ulamuliro. Anati kwa Eva, "ukhoza kutsimikiza kuti sungafe! Pakuti Mulungu anadziwa kuti ukadya chitso cha

ntengowo, matso ako azatseguka ndipo udzaziwa zinthu zomwe sunaziziwepo ndikale lonse... zonse zabwino ndi zoyipa” (Gen. 3:5). Satana anamuuzza Eva bodza. Iye ndi ‘tate wa mabodza’. Eva anatenga zanja lake nathyola chipatso ndi kuchidya. Chinali chipatso chomwe Mulungu anawauza kuti asazadye. Kenako anakapatsa Adamu chipatso ndipo iyenso anadyako. Siku limenero, m’manda okongola wa Edeni, chinthu choyipa kwambiri chinachitika.

Adamu ndi Eva sanamvere lamulo la Mulungu. Mulungu anawalegwa ndi zitsankho, koma Satana anabwera ndikuzawayetsa. Pamene amayetsedwa Adamu ndi Eva anapanga chitsankho choyipa. Anamvera Satana ndikumvomera m’malo mwa Mulungu.

Anapanga choyipa ndipo machismo awo anatembenuza mitimayawo kuchoka kwa Mulungu. Tchimo linawalekanitsa iwo ndi mulengi wawo yemwe anawapatsa moyo. Mulungu anawalora iwo kukhala ndi ufulu osankha kuchita chabwino ndi choyipa. Kumumvera iye kapena kumumvera Satana.

Nkumano wathu ndi Mulungu una onongedwa chifukwa cha tchimo losamvera Mulungu. Timalitchula tchimo loyambirira. Mulungu anaziwa kuti sikwabwino kuti munthu akaziwe tchimo, ndikukhala muyaya opanda iye. Mulungu amafuna kuti munthu azimumvera iye mwaufulu, kusankha kuchita zabwino ngakhala atayesedwa, kumupembedza iye ndiponso kuyanjananaye iye.

Baibulo limatiuza zokhuza tchimo lamunthu kwa Mulungu komanso zokhuza njira ya Mulungu kwa ife yosankha njira yabwino yobwererera kukatamanda ndi kumvera iye mwaufulu, mosakakamidzidwa.

Baibulo limatiuzanso ife zachikondi cha Mulungu kwa anthu ndiponso ndi udani wake pa zoyipa ndi tchimo. Ndi mbiri yayikulu ya chikonde imene imanenedwapo, yachikondi cha Mulungu kwaife posatengera chionongeko, umphawi ndi mantha oyambisidwa ndi machismo anthu. Baibulo limatiuzanso mmene Mulungu anagwirira ntchito ndi miyoyo anthu ngati Adamu, Abele, Enoki, Nowah, Abrahamuh, Isaki, Yakobo, Yosefe, Yudah, Mose, Davide ndi atumiki akuluakulu ndi oweruza a israeli. Kwa anthu awa ‘amapereka njira yobwererera kwa Mulungu kuchoka kunjira zamumdima za tchimo’ kuzera mukupereka nsembe ndi kumvera malamulo achipangano chakale. Kuzera muku badwa, kufa ndi kuukitsidwa kwa Yesu, dziko lonse linapasidwa mwayi odziwa Mulungu kudzera mukulandira nsembe ya Yesu m’malo mwathu ndiponso kumvera mzimu wake Woyera.



‘Eva anaona kuti chipatso chantengowo chinali chabwino kudya... ndipo anadya ndikukapasa china mamuna wake. Kenako iwo anadziwa zinthu zomwe sanadziweko ndikale lonse’. (Genesis 3:6-7)

ADAMU NDI EVA ADZIWA KUTI ANAPANGA ZOLAKWIKWA

Pachiyambi Mulungu analenga dziko ndichirichonse chilimnenemo, ndipo zinali bwino (Genesis 1:10, 21, 31). Panalibwe cholakwika: popanda ululu, popanda kuvutika. Popanda matenda, popanda umphawi, popanda njala, popanda nkhondo, popanda tchimo ndiponso popanda imfa.



M'mene magadzi olungama amabisira tchino:

Lamulo la chipangano chalale cha Mulungu chimati, "munthu amene wachimwa akuyenera kufa". Amayenera chilango ndiponso sakalowa kumwamba pokhapokha atalapa. Adamu ndi Eva anachita cholakwika. Kodi Mulungu anakhala bwanji olungama ndi osakondera ndikuwasiyabe choncho kukhala ndi moyo?

Mulungu anatenga chinyama ndikuchipha. Kenako anawapangira Adamu ndi Eva zovala kuchokera kuchikopa cha nyama (Gen. 3:21). Munjira iyi, Mulungu anagwiritsa ntchito magazi achinyama anapha ija kubitsa tchimo ndi manyazi a Adamu ndi Eva. (Anayesera kubitsa matupi awo ndi zovala zamatsamba.) Mulungu anati sitingabitse tchimo ndi manyadzi athu ndizinthu zopanga tokha. Sitingayeretse machismo athu. Tikuyenera kupempha Mulungu kuti atikhululukire kenako kumuthokodza ndikumukhulupirira panzer yake kutsogoloku.

Mulungu anapitiridza kumpatsa Adamu ndi Eva ndi zidzukululu zawo chikhululukiro chake kuzera mukubweredza kwawo kupeleka nsembe ya magadzi olungama. Mulungu anagwiritsa ntchito nsembe ya magazi achinyama cholungama ngati chionetsero cha njira imene azagwiritsa ntchito nsembe ya magadzi a Yesu pokhululukira machismo kutsogoloku. Yesu anali wolungama. Sanachimweko. Siife olungama koma kuzera mumagadzi ake tingathe kukhululukiridwa. Mulungu payekha angathe kutipulumutsa kumachimo kuzera mwa magadzi a mwana wake. Izi ndichifukwa cha chisomo ndi chifundo ndinso chikondi cha Mulungu. Yesu anatenga chilango chamachimo athu ndikutifela pamtanda kuti tikakhale ndi moyo kwamuyaya ndiye kuzera muchiukiso cha Mulungu. Itapita imfa ndi kuuka kwa Yesu panalibenso nsembe ina ya magadzi olungama.

Yesu anali nsembe yoyenera ya anthu onse ndinthawi zonse. Ngati mukhulupirira kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu, mungathe kukhululukiridwa machismo anu kuzera mwamagazi a Yesu. Werengani zambiri za izi m'baibulo ndinso ndemanga za m'baibulo za Manna publication (uthenga wabwino wa Marko).



Kuzunzika mu kugwa

Zotsatira zakulolera Satana m'munda wa Edeni:

- Ubale wathu ndi Mulungu: Unalekana.
- Ubale wathu ndi ife eni: matha ndi manyadzi.
- Ubale wathu ndi ena: Chiwawa.
- Ubale wathu ndi chilengedwe: Kunyalanyaza.
- Ubale wathu ndi Satana: Kuzunzidwa.

Koma zinthu sizilibwino m'dziko lino masiku ano. Izi zilichonchi chifukwa palibe chinthu chomwe chinayendda bwino ndi Adamu ndi Eva. Amamuopa mulenge wawo, Mulungu. Sanalinso olungama ku tchimo lakusamvera ndipo amachita manyadzi chifukwa anali amaliseche. Anamvera Satana ndikumuvomera (3:16). Satana anali mbuye wawo ndiponso tchimo linawa kakamira. Tchino linaononga dziko la Mulungu ndi ubale wake ndi anthu.

Anali Mulungu mwini analo kuti Satana ayetse Adan ndi Eva. Mulungu anafuna anthu kuti azitsankha mwaufulu ndimwanzeru pakati pa zabwino ndi zoyipa. Adamu ndi Eva analephera yeserori ndikusankha kusangalasa iwo eni m'malo mosangalasa Mulungu. anakhulupirira bodza la Satana m'malo mwa choonadi cha Mulungu.

Adamu ndi Eva anadziwa kuti anachita cholakwika. Anadziwa kuti anamuchimwira Mulungu, ndipo sankamva bwino mkati mwawo. Anadziwanso kuti anali maliseche ndipo anafuna kuzivindikira okha ndikubitsira Mulungu matupi awo (3:7-8). Tsopano anali 'akapolo atchimo'.

Mulungu anatipatsa njira yodziwira pamene tikulakwitsa. Sitimamva bwino mwaife. Chinachake mwaife chimaitana chikumbumtima chimene chimatiuza kuti "tapanga zolakwika". Mulungu anatilenga ndichikumbumtima chimene chimatithandiza kujdziwa chabwino kuchoyipa.



Lankhulani za izi:

1. Chifukwa chiyani Mulungu analenga onse mamuna ndi mkazi?
2. Chifukwa chiyani Mulungu anatilenga muchifaniziro chake?
3. Chifukwa chiyani Mulungu analola satana kuyesa Adamu ndi Eva?
4. Ndi chiyani chimene Mulungu anatipasa kuti chitithandize kuchita zolondola?
5. Kodi Mulungu anapanga chinthu chimene sichinali chabwino?



Ganizirani za izi: Mulungu amalola Satana kuti atiyese. Mulungu ndiwachilungamo potipasa chisankho chazabwino ndi zoyipa? Kodi ndindani amalamulira moyo wako? Timazunzika bwanji tikasankha choipa?

ANAYESA KUBISA MANYAZI AWO

Mulungu anapanga Adamu ndi Eva Angwiro. Anawapanga muchifaniziro chake. Koma sanamvere Mulungu ndikudya chipatso chantengo wachabwino ndi choyipa.

Mulungu anapanga chotheka kuti Adamu ndi Eva azipanga moyo kuzera mukukhala ndi ana. Koma atachimwa, maso awo anatsekuka. Anawona matupi awo amaliseche ndipo anayetsa kubisalira Mulungu. Anadziwa kuti analakwisa. Umaliseche wawo unawalekanisa ndi Mulungu. Anthu amasiku ano anasangalala ndi umaliseche m'malo mosangalala ndi Mulungu. Ana athu amapangidwa modabwitsa ndi mphavu kulenga ana. Koma tikuyenera kumalambira ndikusangalala ndi mulengi wathu wodabwitsa, osati matupi athu odabwisa!

Adamu ndi Eva anapeza matsamba aakulu nawatsoka limodzi kupanga chovala. Anayesera kubisa umaliseche wawo poziphimba umaliseche wawo ndi masamba. Anavala masamba ndikukabisala munkhalango. Anadziwa kuti Mulungu

abwerera ndikuzayankhula nawo. Ankabwera nthawi zonse chakumadzulo kukudzidzira (3:8). Anabwera? Anatsiya kuwakonda? Ayi! sanatsiye kuwakonda koma anali okwiya. Pamene sitimvera Malamulo a Mulungu zimamuwawa, zimatiwawa ife ndiponso zimawawa anthu ena.

Chakumadzulo, Mulungu anabwera kumunda kuja kuzayankhula ndi ana ake. Kupusa kwanji kwaiwo kuganiza kuti angabisalire Mulungu! Baibulo limati "Palibe angabisalire Mulungu. Maso ake amaona chilichonse timachita. Tizayankha kwa Mulungu pazimene timachita" (Ahebri 4:13).

Pali njira imodzi yokha kwa anthu amene analekana ndi Mulungu kuti abwerere kwa iye. Akuyenera kuzimvera chisoni pa tchimo lawo lochita zolakwika. Akuyenera alape. Akuyenera kutembenuka kuzinthu zolakwika zomwe amapanga ndi kubwerera kwa Mulungu wawo wakumwamba.

Mulungu anafuna kuti Adamu ndi Eva avomeredze tchimo lawo ndikuzimvera chisoni posamumvera Iye lamulo lake. Anafuna Adamu kuti aulule tchimo lake, choncho Mulungu anabwera ndi kudzayitana Adamu, "ulikuti" (Genesis 3:9).

ZOSATIRA ZA ZOCHITA ZOYIPA

Adamu ankaopa. Sankafuna kuti Mulungu amupeze. Ankawopa kukumana naye Mulungu. Tchimo limawononga ubale wathu ndi Mulungu.

Anthu amafunsa, "Chifukwa chiyani Mulungu analenga dziko ndimachimo ochuluka chotere ndimatenda ndi kudzudzika mkati mwake masiku ano?" yankho ndiloti Mulungu analenga dziko la ngwiro. Mulungu anati chilichonse anachilenga chinali chabwino kwambiri. Koma anthu anachita zoyipa, ndipo tchimo linasanduka tate wawo. Ndiwochimwa ndipo tchimo limaletsa anthu kumvera Mulungu. Zimabweretsa mkwiyo ndi nkondo komanso kuwononga ubale wathu ndi Mulungu ndi anzathu.

Njira zathu zoyipa zinasintha dziko kukhala malo achisoni ndi mavuto. Paulo ananena m'baibulo kuti "anthu onse anachita zoyipa ndipo anthu onse ali kutali kukhala abwino ngati Mulungu" (Roma 3:23). Izi zinachitika chifukwa Adamu ndi Eva sanamvere Mulungu. Ichi ndichifukwa chake ankristu amakhulupirira kuti tonse timabadwa ndi tchimo m'moyo wathu. Siife angwiro.

Mulungu sanayiwale zokhuza Adamu and Eva, kapena dziko lokongola lomwe analilenga. Amayitana anthu onse kuti asiye machismo awo ndikuti abwerere kwa iye. Anthu ambiri safuna kusaka Mulungu koma Mulungu amatiyitana ife. Amafuna kuti tikhale anzake.

M'munda wa Edeni, Mulungu anayitana, "Ulikuti Adamu" ngakhale kuti Mulungu amadziwa kumene Adamu anali. Anadziwa kuti Adamu ndi Eva anabisala.

Mulungu amafuna Adamu abwere kwaiye ndikukamuuza chomwe anachita molakwika. Anafuna kukhululukira Adamu ndi Eva pazimene anachita ndikukhalanso pachinzake kachikena. Koma iwo sanavomereze tchimo lawo mmoyo wawo (3:12-13). Anakanilana wina ndi nzake. Eva anati linali vuto la njoka ndipo Adamu anati linali vuto la Eva ndiponso kumuyimba mlandu Mulungu

pomuypa Eva ngati mkazi wake. Tchimo limapanga zimenezo: tchimo limodzi limazetsa tchimo lina.

Baibulo limati tisayimbe mlandu ena pazinthu zoyipa zomwe tachita. Sitingayimbe mlandu makolo athu, ngakhale kunena kuti takulira mbali yosauka ya dziko, kapena kuti tinali ndi anzathu oyipa pamene tinali ana. Mulungu amati "munthu aliyense akuyenera kuyankha..." (Mateyu 12:36). Tiri ndi udindo pacholakwika chilichonse.

Chifukwa Mulungu ndi wowona ndi wachilungamo, akuyenera kulanga tchimo. Choncho Mulungu analankhula kwa njoka. Anati, "chifukwa wachita izi, ndukukutemberera. Ndiwe otembereredwa kupotsa nyama zina zonse ndizinyama zakutchire. Uzakwawa pansi. Uzadya fumbi masiku onse amoyo wako. Ndiyika udani pakati paiwe ndi mkazi. Ana ako ndi ana amkazi adzakhala pa udani. Koma ana ake azaphwanya mutu wako. Ndipo iye uzaphwanya chidendene chake (3:15).

Izi zikutanthauza lonjezo la Mulungu kuti sikulina mwana chapaderadera wa chidzukululu cha Eva azaphwanya ndikugwetsa Satana. Timakhulupirira kuti izi ndi umboni wakubadwa kwa Yesu Khristu, mwana wa Mulungu, kukonzedwa kuchoka pachiyambi ndi Mulungu kuti abweretse chipulumutso ndikumvera kwamunthu ndi ulemelero kwa Mulungu. Mulungu atate wathu kudzera mwa Mzimu woyera anawonekera Maria, kudzalenga mbewu yakubadwa kwa mwana wake, amene anali kumwamba kuyambira pachiyambi. Yesu anakhala munthu opanda tchimo amene anadzudzika ndi kufa kulandira chilango chotiyenera ife. Izi zinachitika pamene Yudasani anamupereka Yesu, kukaniritsidwa kwa tanthaudzo la 'kuphwanya chidendene chake'. Chisomo chodabwitsa.

Kenako Mulungu Atate anati kwa Eva, "ndiyenjezera ululu wako poeleka. Udzakhala muululu pamene udzidzakhala ndi ana. Uzazipereka kwa mamuna wako. Ndipo adzalamuliraiwe" (3:16).

Mulungu Atate anati kwa Adamu, "wamvera mkazi wako. Wadyachipatso chantengo umene ine ndinakulamulira iwe zaiwo. Ndinati, 'usazayerekeze kudya chipaso chake.' Choncho ndikukutemberera iwe pansi. Udzadya zomera zakumunda, ngakhale nthaka imatulusa minga ndi mutual. Ukuyenera kuzagwira ntchito molimbika ndikutuluka thukuta kwambiri kuti ukakolole chakudya choti udye. Unapangidwa kuchokera ku dothu, ndipo uzabwerera kuilo. Ndiwe fumbi ndipo kufumbi uzabwerera" (3:17-19).

KUTULUTSIDWA M'MUNDA MWA EDENI

Choncho Mulungu anatulutsa adami ndi Eva mmundawo ndikuseka njira yake yobwererera. Mulungu analanga anthu onse chifukwa cha tchimo la Adamundi Eva pakuwatulutsa mmunda wa Edeni (3:23). M'ngero wamphavu amalondera njira yobwerererawo ndi mpeni wamoto (3:24).

Limenero linali siku loyipitsitsa kwambiri mu mbiri ya dziko lapansi. Ululu ndi kugwira ntchito molimbika kunasanduka mbali yamoyo.

Kuyambira sikulimenero, Adamu amayenera kulimbikira ntchito ndikugalauza nthaka kuti apeze zakudya zokwanira. Ndipo nthawiiriyonse Eva amabeleka

amamva ululu. Zonsezi zinali gawo la themberero limene linabwera kwa mamuna ndi mkazi chifujwa cha zochimwa zawo. Tchimo limabweretsa mavuto nthawi zonse. Tchimo limayambitsa ululu ndi kudzudzika kwa ife. Tchimo likuyenera kudulidwa ndiochimwa aliyensa asanalowe kumwamba.

NJIRA YA MULUNGU YOTIRETSA KUCHITA ZOYIPA

Akamakhala kuti Mulungu analangiiratu kotheratu Adamu ndi Eva, akanakhala atafa (2:17). Ndiponso sitikanakhala pano lero! Mulungu ndi Mulungu woywra ndipo samalora tchimo. Choncho Mulungu anapeza njira zina zothandizira anthu kukhala achoonadi kwaiye, mupewa chilango ndikukwaniritsa cholinga chachilengedwe chake. Baibulo limatiuza za anthu akale omwe ankamvera Mulungu. Mwachistsanzo, Nowah, Abrahamu, Isaki, Yakobo, Mose, Davide... omwe tiwerenge za iwo nyhawi ina. Ndiponso baibulo limatiuza za njira ya chipulumutso cha Mulungu kwa onse amawayitana ndipo amamumvera iye.



Chilungamo cha Mulungu mu Genesis mutu 3

Muli zirungamo zofunikira zimene Genesis mutu 3 amatiphunzitsa:

- Tchimo loyambirira ndiko kusamvera Mulungu (v.6).
- Khalidwe lochimwa la Adamu ndi Eva lakhala ndikupitirirabe mwa ana awo ndi anthu onse adziko lapanso (Romans 3:23).
- Satana azakhala pankhondo ndi anthu onse (v.15).
- Azimayi azamva ululu pobereka (v.16).
- Azimayi azazipereka kwa amuna awo (v.16).
- Mamuna akuyenera kugwira ntchito molimbika kuti akhale ndimoyo (v.17).
- Nthaka izawirira ndi tchire (v.18).
- Nthaka izapereka chakudya chokwanira kukhalira ndi moyo ngati tilimbikira (v.18).
- Matupi awanthu azafa ndikusakhalanso ndi moyo kwamuyaya (v.19, 22).
- Mulungu analola chikopa cha nyama kugwiridwa ntchito kuvala (v.21).

Lerolino, anthu amene safuna kukhulupirira Mulungu akuyesera kusintha kapena kusagwirizana ndi zinthu izi.

Ziwani kuti zinthu izi ndi mbali yachilango chauchimo chomwe Mulungu anachilola:

- Ululu pobeleka (v.16).
- Tchire kumera limozi ndichakudya (v.18).
- Ntchito yolemesa kuti tikakhale ndi moyo (v.17-19).

Izinso ndi zilango za Mulungu:

- Mana wa mamuna wamunthu wamkazi "azanyenya mutu wa Satana" (v. 15). Iyi ndi nthawi yoyamba Mulungu kunena za kubwera kwa Mpulumutsi (Yesu Khristu, obadwa mwa Maria).
- Munthu azizadya chakudya chomwe wachigwirira nchito "m'masiku onse amoyo wako" (v.17-19) ngati agwira ntchito molimbika.

Baibulo limatiudzanso zokhuza anthu oyipa amene amayambisa mavuto mu dziko lomwe iye analilenga. Ichi ndichifuka chimene Mulungu analonjedzera zotumiza mpulumutsi (3:15). Anayitana ndi kuzoza anthu abwino ochuluka kuti alodzere njira yobwereraera kuchoka kumachimo kwa zaka zikwizikwi. Anapereka malamulo ndikusankha nsembe ya mwadzi wa nyama kuti akalimbikise kulapa ndi kumvera ndiponso kupembedza. Kenako siku lina, panthawi yokhazikika kwa Mulungu, Yesu anatenga chilango chamachimo a dziko lapansi (1 Peturo 2:24, 3:18). Mulungu anatumidza mwana wake, Yesu Khristu. Yesu anabwera kuzachotsa zonse zinali zolakwika mumitima ya anthu. Anabwera 'kuzayang' a ndikupulumutsa osochera' (Luka 19:10). Pakuti Mulungu anati "Onse anachimwa..." (Aroma3:23). "Mulungu anali mwa Yesu, mwana wake. Amagwira ntchito kuzera mwa Yesu kuti abwezeretsenso dziko lonse kwa iye mwini" (2 Akolinto 5:19).

Pamene Adamu anachimwa, anapasira khalidwe lake lochimwa kwa ana ake. Ndipo nawo anapasira ana awo khalidwe lomwero lauchimo kwa ana awo. Dziko lonse linasokonekera mutchimo ndikulekana ndi Mulungu. Choncho Baibulo limati, "palibepo ndimmodzi yemwe ali oyera kwa Mulungu. Palibe, ngakhale mmodi" (Masalimo 14:2). Ndife tonse ochimwa. Nsembe yokhayo ya mwadzi ndi nsembe yomalidza ya Yesu inali yokwanira kubwezeretsa munthu kwa Mulungu.

NJIRA YOBWERERA KWA MULUNGU

Chifukwa ndife ochimwa ngati Adamuu, timazibitsa kwa Mulungu. Timayetsera kuvindikira machismo athu. Timawanamizira ena. Chifukwa chayani izi? Chifukwa tiri ndi kwalibwe lochimwa la Adamuu mkati mwathu. Tiri ndinjira zake zochimwa. Sitimvera Mulungu ndiponso mitima yathu inachoka kwa iye. Ife sitiri angwiro. Ndipo Mulungu anachenjedza Satana kuti Iyr azapambana nkondo yolimbana ndi tchimo (Gen. 3:15). Yesu, amene sanachimwepo anafa kuti akhale nsembe yangwiro kwa anthu ochimwa.

"Tidali ofooka ndipo sitikanatha kuzithandiza tokha" (Aroma 5:6-8). Kenako Yesu anabwera munthawi yoyenera ndikuzapereka moyo wake kwa ochimwa. Anapereka moyo wake m'malo mwa moyo wanu ndi machismo anu.

Iye adzachotsa machismo athu kuti ubale wathu ndi Mulungu ubererenso. Kenako tingathe kuzalankhulana naye ngati Adamu ndi Eva kumayambiriro mmunda muja. Iyi ndinjira yachipulumutso cha Mulungu. Cholinga chake chinali choti amuna ndi akazi "akakhulupirire mwa Yesu Khristu ndi kupulumutsidwa" (Ntchito 16:31). "Ndinthenga wabwinowu munapululumutsidwa" (1 Akolinto 15"2). Nthawi zambiri chimatchedwa 'chinsisi cha Khristu'.

Ngati mukhulupirira Yesu ngati mpulumutsi wanu, muzakalowa kumwamba mukazafa. Lolani Yesu akuwomboleni kumachimo. Pemphani Mulungu kuti akukhulukireni. kenako pitirizani kuwelenga m'baibulu zokhudza cholinga Cha Mulungu kwa aliyense mwa Yesu khristu. Muzapeza chitsangalalo ndi mtendere mukamakhala muchiyero ndi Mulungu. Mulungu wathu wamphavu zonse, Yahweh, amene analenga dziko, adzakuthandizani ndipo azakhala m'dzanu.



Lankhulani za izi:

1. Ndichifukwa chiyani timati anthu ochimwa analekanisidwa ndi Mulungu?
2. Ndichifukwa chiyani timati anthu ndiochimwa kuyambira pobadwa?
3. Kodi munthu ochimwa angabwererense bwanji kwa Mulungu lero?
4. Kodi Mulungu woyera angakhulukire bwanji munthu ochimwa?
5. Kodi lamulo labanja la Mulungu ndiriti (Gen. 2:24)?



Ganizirani za izi: Kudzera muchilango chamulungo cha ululu pobereka, kubwera kwa moyo watsopano; chilango chogwira ntchito molimbika zimabweretsa moyo.



Kuwerenga Baibulo: Genesis mutu 4 ndi 5



Phunzira za izi: *kubagwa kwa Kaini ndi Abele ndi kupembedza kwawo Mulungu (Gen. 4:1-7); mmene Kaini anaphera Abele ndi chilango chomwe analandira (8-16); M'bado wa Adamu ndi Eva (v. 17-26 ndi Mutu 5).*

ADAMU NDI EVA AKHALA NDI MWANA

Adamu ndi eva anali bambo ndi mayi. Munthawi imeneyo Mulungu anatipasa lamulo la banja ndipo silinasinthepo. Lamulo la banja la Mulungu limati, "Mamuna azasiya bambo ndi mayi ake, ndikukalumikizana ndi mkazi wake. Ndipo awiriwo azakhala mmodzi" (2:24).

Mulungu anapanga lamulo lachilengedwe. Anayika nyenyedzi kuti izisatira njira yake. Sizingoyenda paliponse mulengalenga. Zimayenda munjira yoyenera. Dziko lonse ndilozaza ndi dongosolo la Mulungu. Dongosolo lamuchilengedwe limasatira lamulo lachilengedwe. Pamene ndagwa muntengo, ndimagwera pansu, osati mmwamba! Ili ndilimodzi mwa lamulo la Mulungu lachilengedwa. Timalitchula kuti mphavu yokoka. Malamulo a Mulungu onse ndi abwino kwaife. Ndipo lamulo la banja la Mulungu ndilofunikira kwambiri. Ndilabwino kwaife.

Mamuna siokwanira popanda mkazi. Mkazi siwokwanira popanda mamuna. Aliyense amafuna nzake. Ukwati pakati pa mamuna ndi mkazi ulibe vuto chifukwa ndiwoyenera. Chimenecho ndicholinga cha Mulungu. Limenelo ndi lamulo la Mulungu. Ndiloperekedwa ndi Mulungu. Mmenemo ndimene timachulukira mdziko kuti tikakasangalale ndikuthokodza pa zomwe anazilenga.

Mulungu anaudza Adamu ndi Eva kuti atenge ulamulilo kudziko lapansi (3:23) ndikulisamalira. Anali ndi ntchite yoti azigwira. Sakanatha kuchita zimenezi mwaiwo okha; anafuna ana kuti awathandidze. Ndipo amayenera kuwaphunzitsa anawo zokhunza Mulungu. Mulungu amafuna dongosolo mumabanja mwathu.

Adamu anagona ndi mkazi wake. Anakhala ndi pakati ndikubeleka Kaini (4:1).

Zitangotha izii, Adamu ndi Eva anakhalanso ndi mwana wina ndipo anamutha Abele (4:2).

Mulungu analenga adamu ndi eva muchifanidziro chake (5:1). Koma ana a adamu ndi eva anabanga ochimwa monga anthu. Monga iwo, mitima yathu imatembenukira ku zoyipa. Munthu yekhayo anabagwa monga Mulungu anali



Kugonana, Ukwati ndi Chisudzulo

Mulungu anapanga lamulo limodzi lokha la banja. “Mamuna azasiya bamboo ake ndi mayi ake ndikukalumikizana ndi mkazi wake. Ndipo awiri ayiwo azakhala mmodzi” (Gen. 2:24). Limenelo ndilamulo labwino. Ndipo anthu akasunga lamulo la Mulungu la banja lizakonza mavuto ambiri. Mulungu anaziwa kuti mamuna amafuna mkazi. Ndipo anaziwa kuti ana amafuna abambo ndi amy. Lamulo lake limadalitsa mamuna ndi mkazi ndiponso limatetedza banjalo.

Choncho ndicholinga cha Mulungu kuti mamuna ndi mkazi akwatilane. Ndicholinganso cha Mulungu kuti iwo azikhala ndi ana pamene akwatilana. Anakupanga chisangalalo “kupanga chikondi” kuti ana akabadwe. Ngati kusangalala popanga chikondi sikunali kwabwino ndekuti ana sakanakhalapo ndiponso munthu akanafa osazapezekaponso.

Koma ngati tisaka chisangalalo mukugonana popanda ukwati kumeneko ndikutsusana ndi cholinga cha Mulungu. Komanso ngati tikhala ndi ana tisanakwatirane, zithakuyambitsa mavuto ndi kukhumudwa kwa ana. Ngati tigonana munjira ina ndekuti chimenecho sicholinga cha Mulungu. Ngati mamnu akhala ndi akazi ochuluka, zimayambisanso nsanje ndi kukhumudwa. Ngati mamunu asintha mkazi wake ndi wina, pamakhala mkwiwondi kukhumudwa ndiponso kusokonekera kwa ana. Yesu amaziwa kuti ndicholinga cha Mulungu kuti mamuna azikhulupirika kwa mkazi wake, kusakhanso ndi wina aliyense ndikukhala ndi mkazi wake mmodzi yekhaya ngati ndikotheka moyo. Munjira iyi, ana angathe kubadwa ndi kukula pakhomo lachikondi osati okhumudwa ndimakolo amene sakukhulupirika kwawina ndi nzake. Yesu anati ichi chinali cholinga cha Mulungu kuchokera pachiyambi (Mateyu 19:18). Kulekana ukwati ndicholinga cha mamuna.

Anthu ena omwe anakwatirana sakhala ndi ana. Kumbukirani kuti ngati mulibe ana mubanja, ukwatiwo ndiwokwanirabe. Munalibemo kuchula za ana mu Genesis 2. Choncho sikwabwino kuthesa ukwati chifukwa mulibe ana. Ndiponso ndizolakwika kwa anthu kunena kuti banja likuyenera kukhala ndi ana. Banja ndilokwanira ngakhale ana mulibemo. Ngati mamuna ndi mkazi wake afuna chisangalalo mukugonana osakhala ndi ana ndizabwinobwino. Kupanga chikondi ndi mphatso yochokera kwa Mulungu.

Kuteganso mwana oti alibe amakolo kungakhale kwabwinonso.

Choncho ukwati pakati pamamuna ndi mkazi ndilamulo la Mulungu. Koma kuthesa ukwati ndilamulo la munrhu. Lamulo la Mulungu silingaphwanyike popanda wina kuvulala. Zimenezo ndizoona zake za kuthesa ukwati ndizoona zake zokhuza kugonana kunja kwa ukwati.

Amuna asakakamize akazi awo kuchita nawo zachikondi. Akuyenera kukonda nzake kuchokera mumtima ndikupanga chikondi ngati mmene Baibulo limanenera, kuganizirana wina ndi nzake. (Welengani nyimbo ya Solomoni).

Kusamvera malamulo a Mulungu pa kugonana ndi ukwati ndikupana chikondi munjira yoti sichinali cholinga cha Mulungu pachiyambi kukhonzanso kuzetsa ifa yachangu, osati moyo. Yesu anatischenjedza kale ife kuti tisamalole kugonana kosayenera kuti tiyipise ntchito yabwino ya chilengedwe cha Mulungu ndi chifundo (Chivumbulutso 2:22)

Macharichi ena amati a nsembe asamakwatire, koma kusalola ukwati ndikolakwika (Gen. 2:18; 1 Timoteyo 4:3). Komabe tingathe kusankha osakwatira.

mwana wake yekha, Yesu Khristu. Yesu anabagwa kuzera mwa mzimu woyera wa Mulungu mwa virigo Maria. Yesu anabadwa ngati munthu koma opanda tchimo lobadwanalo. Ndipo sanalolere kugonjera mayeselo. Ndipo sanakhalepo osamvera Atate ake, Mulungu wamphavu zonse.

MOYO KUNJA KWA MUNDA WA EDENI

Ndikhulupirira kuti Adamu anawuza ana akeawiri za munda wa edeni ndi zinthu zomwe zinachitika kumeneko, mmene Mulungu anawatulusira iye ndi mayi awo mmundawo chifukwasanamere malamulo ake. Sopano anadulidwa ku moyo wapadera wa Mulungu mu munda wa nthaka. Edeni anali kale lawo ndipo sizikanatheka kuti aberere (3:23).

Mulungu anayika angelo amphavu ndi malupanga a moto kyti aseke njira (3:24). Chinali chithunzithunzi cha chiwerudzo cha Mulungu ku tchimo, ndiponso themberero lake pa Satana ndo zoyipa zonse. Pazakhala nkondo pakati pa omwe amasatira Satana ndi omwe ali ndi chikhulupiriro mwa Mulungu (3:15).

Pamene Adamu anachimwa ndikusamvera Mulungu, malingaliro ake ndi mtima wake zinachoka kwa Mulungu. Tchimo linasintha chikhaliidwe chonse cha Adamu. Chosakhala bwino ndichoti Adamu anapasira ana ake khalidwe lake lochimwa ndipo iwo anapasira ife. (Asroma 5:12). Tonse tiri ndi chikhaliidwe chochimwa cha Adam! Tonse tinachimwa kuzera mwa Atate athu Adam ndipo khalidwelathu limatiramulira. Popanda mzimu wa Mulungu mmoyo wathu, tchimo ndiye tate watu! Chifukwa choti tchimo ndi tate wathu, timapanga zinthu zoyipa. Mawu a Mulungu kwa paul anati, "onse anachimwa..." (Aroma 3:23)

Maganizo athu amatikumbusa za tchimo koma chikhumbokhumbo chathu chikuyenera kukha kwa Mulungu. Ichi ndi chifukwa chimene tikuyenera kumvetsetsa cholinga chachikulu cha Mulungu chotipulumusa. Mulungu anavomera nsembe ya Yesu chifukwa chamachimo athu. Kulibenso njira ina yobwerera kwa Mulungu kuchokera ku mdima wamachimo kuti tikakhale ndi moyo woyera mukuwala kwake ndi chilungamo chake.

Pamene Kaini ndi Abele anali ana, amagwira ntchito ndi makolo awo kuminda. Anaphunzira mmene angagwiritsire ntchito nthaka pobzala bewu ndikusamalira ziweto.pamene amakula, Kaini anasankha kubzala zakudya. Abele anasankha kugwira ntchito ndi nkhoa. Mamawauliwonse, amazitulusa kukasaka udzu. Madzulo amazibweresa ndikusazisiya malo otetezeka.

KAINI NDI ABELE AYESA KUPEZA NJIRA YA MULUNGU

Tsiku lina, Kaini ndi Abele anabweresa nsembe kwa Mulungu. Zinali zoti awonese kuti akufuna kupembeza iye ndipo anabweresa mphatso zawo kuzamuthokoza.

Mmawa umenewo Abele anapita kukasaka ana a nkhoa wabwino kuti apereke nsembe kwa Mulungu. Anali oyamba kubadwa ndipo anali ana a nkhoa a amuna (4:3). Anawapha ndikukonza nyama yake pa guwa. Kuphatikizapo mafuta ake amene anamusangalatsa Mulungu.

Kaini anadula bewu zamasamba zakucha ndikuzibweresa paguwa la banja. Kaini anali osazikayikira. Anafuna kupembedza Mulungu munjira ya keyake.

Baibulo limatiuza, "Mulungu anakondwerese gwa ndi nsembe ya Abele. Koma sanakondwere ndi nsembe ya Kaini" (4:5). Kaini anakwiya ndipo anali ngi mkangano ndi Mulungu pa zimenezi. Choncho Mulungu analankhula ndi Kaini ndikumpasa mwayi oti absinthe maganizo ake. Mulungu anayita Kaini kuti alape ndikuti achite zokondweresa Mulunguyo.

Mulungu amasendera chifupi nafe ndi chisomo ndi chifundo, ngakhalenso timachita zolakwika. Chikondi ndi kukondera kwake kumakhala kwa ife nthawi zonse. Pamene Mulungu watiyitana timakhala ndi zisanko ziwiri. Tikhonza kukhulupirira iye ndi kumvera iye kapena ayi! Tonse timayenera kusankha. Anthu anamva ndi kumvera mawu a Mulungu, kapena kumvera mawu awochimwayo mumitima mwawo. Pamene achoka pa mawu a Mulungu ndikuyenda njira zawo, Mulungu amakwiya. Amawalola kuti akakumane ndi mavuto choncho kuti akamumvere iye, koma sawakakamiza kumvera iye.

Kaini anaganiza kuti angamvere Mulungu munjira yake, koma Mulungu anamuchenjedza, "ngiti muchita chimene chili cholondola Mulungu azalandira" (4:7). "Tchimo limakhala pakhomo kudikirira kulamulira inu".

Kaini anaphunzira kuchokera kwa Makolo ake kuti chilichonse timachita, pamakhala njira yabwino ndi yoyipa. Kodi tingaziwe bwanji chimene chiri chabwino? Mulungu anatiwuzza mmawu ake. Mawu ake ndi achilungamo. Mungathe kukhulupirira mawu a Mulungu! Anati pasa ife nthumazi. Anapasanso omukhulupirira mzimu woyera kuti uziwasogolera.

Koma Kaini anakana njira ya Mulungu yopanjira zoyenera. Kenako anabwera mkwiyo. Moyo wake unayipisidwa ndi tchimo. Anasanduka kapolo watchimo.

Mulungu anadikira Kaini kuti alape. Ngiti Kaini akanapepesa, Mulungu akanalandila kupembedza kwake kowona. Kaini anaziwa kuti Mulungu sanakondwere ndi zopereka zake. Koma sanafune kupereka zomwe Abele anapereka. Sanafune kupempha mchimwene wake mwana wa nkhusa kuti apereke nsembe kwa Mulungu. Sankafuna kupempha. Ankadziwa chomwe chinali choyenera kusangalasa Mulungu koma analephera kuchitga. Sanamvere Mulungu ndikukhala ndi nkwiyo.

Kaini anakwiyiranso mchimwe wake. Zimenezo sizinali zabwino. Silinali vuto la Abele, linali vuto la Kaini.

"Chifukwa chani wakwiya?" Mulungu anafusa. Mulungu anamuza Kaini, "panga zomwe zili zoyenera" (4:7). Baibulo limati: "Mwachikhulupiriro Abele anapereka zopereka zabwino lkwa Mulungu kuposa Kaini" (Ahebri 11:4), komanso "musakhale ngati Kaini amene anali wakwaoyipawo [Satana]"¹ Yohnane 3:12).


MULUNGU APASA KAINI MWAYI WINA

Mulungu anamulamula Kaini kukhala ndi chikhulupiriro mwa iye ndi kuvomerezedwa. Mulungu anati, "ngati supanga chomwe ndichoyenera, ychimo likukudikira pakhomo kuti likugbwire. Koma ukuyenera kuti uliramulire" (Gen. 4:7).

Kaini anaziwa chomusangalasa Mulungu. Anaziwa kuti nsembe ya nyama inali yovomerezeka kwa Mulungu. Koma m'malo mwake anakwiya ndipo sanapemphe mwana wa nkhusa kuti apepeke nsembe.

Ali Kunja kwa Munda, Kaini anapha mchimwe wake chifukwa chosatha kulamulira nkwiyo wake (4:8). Nkkwiyo uli ngati moto. Umawotcha mkati mwa mtima wa munthu.

Mulungu analankhula kwa Kaini. Ooh, chifundo ndi chisomo cha Mulungu! Mawu ake okoma amakhala akubwera kwa ife ochimwa nthawi ndi nthawi. Ooh, chisomo cha Mulungu kuti sayenda njira zake ndikutisiya ife tikuzuzika ndi machismo athu.



“Alikuti mchimwene wako?” Mulungu afusa Kaini.

Kachikenanso Kaini amayenera apnge chisankho. Akanatha ku ulula ychimo lake ndikupempha chikhululukiro. Koma anasankha kupewa fuso la Mulungu ndi kunena bodza kuti abise zimene anachita. Kupusa kwanji! Mulungu amaziwa zonse za ife, ndipo amadziwa zones za Kaini! Amawona mkati mwa mitima yathu ndi miyoyo yathu (Ahebri 4:12-13).

SATANA, TATE WA ONAMA

Choncho Kaini anatengera Adamu ndikusankha kuchita zoyipa. Mpakana Satana anayika kupha mumtima mwake. Yesu anati, onse osatira Satana ndi ana a chiwanda' (Yohane 8:44). Satana ndi tate wa onama.

Mulungu anapasa Kaini nthawi kuti alape ndi kuwulula tchimo lake. Anawuza mlungu kuti samadziwa komw mchimwe wake anali. “ndimayenera kuti ndiziyang'anira mchimwene wanga?” (Gen. 4:9). Kuyambira pachiyambi mpaka kumapeto, Baibulo limayitana anthu kuti alape ndi kuvomereza machismo ake kwa Mulungu (4:10). Mulungu amadikirira kuti tichite izi koma sadikira mpaka kalekale.

Pamene Mulungu amayankhulanso ndi Kaini, chinalino chiweludzo. Ngati sitimvera mawu a Mulungu pamene watyitana ife ndi kukhulupirira iye, nde chasalanso ndichani kwa ife? Chiweludzo chake chokha! Mulungu anayita Kaini, “mwadzi wa mchimwene wako ukundiririra ine kuchokera pansu” (4:10).

Kaini anaweluzidwa chifukwa cha tchimo lake kwa Mulungu, opereka moyo, ndiponso kupha Abele, mchimwene wake, amene anapangidwa muchifaniziro cha Mulungu. Mulungu anamuza Kaini, 'ukamagwira ntchito yako yapanthaka, siizakubwereseranso iwe zokolola. Uzakhala munthu osapuma, uzizangoyenda yenda padziko' (4:12).

'Ndizoposa zomwe ndingakwanise', Kaini anatero. Anakanika kuvomereza kuti anachimwa ndipo amayenera charango. "Lero mukundithamangisa kumalo kuno. Ndizizambisslira inu. Ndizakhala munthu osakhazikika amene azizangyenda ndi dziko. Aliyense amene azizapeza ine azidzafuna kundipha". Koma Mulungu anati, "ayi. Aliyense azaphe iwe azalangidwa kasanu ndikawiri" (4:14, 15). Mulungu anayina chizindikiro pa Kaini. Kenako aliyense omupeza iwe amamusiya uti asamuphe.

Choncho Kaini anachoka kwa Ambuye ndikupita kudziko lina kummawa kwa Edaini kumene palibe amamuziwako. Iye ndi mwana wake wamamuna anamanga mzinda kumeneko (4:17). Kaini anautchula dzina la mwana wake Enoki.

Kaini anapanga chiyambi chasopano muphavu zake ndi mnzeru zake. Amuna a m'banja la Kaini anaphunzira sayansi, luso ndi umisili (4:21-22). Anamwazikana mwachangu kuposa ana a Sefi (mwana wa Adamu wachitatu), amene anali anthu aMulungu. Mtundu wa Kaini sunkasamala za malamulo a Mulungu ndipo amuna ena anayamba kumatenga akazi ochuluka. Bansi pa lamulo la Mulungu mamuna akuyenera kukhala ndi mkazi mmodzi (2:24), koma Lameki anakwatira akazi awiri (4:10).

M'bado wa Kaini unali ochenjera koma osakonda Mulungu. Amakonda zinthu zamdziko lapansi zomwe Mulungu anazilenga koma samakonda Mulungu, mulrnge wa zinthu zonse (Aroma 1:18-25).

Komabe, panali nthawi zina pamene anthu amafuna kubwereranso kwa Ambuye Mulungu ndikukamupembedza iye (4:26). Tipemphere kuti izi zichitike lero nthawi isanatithere. Nthawi idakalipo, Yesu asanabwerenso kachikena kudziko lapansi.

OCHEPA ANAFUNA KULAPA

Adamu ndi Eva anali ndi ana a amuna ndi a akazi ochuluka (5:4). Munthawi imeneyo Mulungu amalola kuti mchimwene ndi mchemwali akhonza kukwatirana kuti akachulukise dziko popanda mavuto la kusintha limene linachitikabe pambuyo pake.

Mulungu anachitira chifundo Adamu ndi Eva ndikuwapasa mwana wammuna Sefi (4:25; 5:3). Unali m'bando wa Sefi umene Enoch wosinthika anabadwira komanso Nowah, onse ayiwo amene amakulupirira Mulungu wamphavu zonse (5:24; 6:8). Choncho Mulungu anatumidza anthu achikhulupiriro kuti azayankhule m'malo mwa iye, koma nthawi zambiri palibe ndi mmodzi amafuna kumva zokhudza Mulungu wamphavu zonse kapena kulapa machismo awo. Tapeza kuti:

- Kunalibeko olapa mumatsiku a Enoch mwana wa Sefi, mwana wachitatu wa Adamu ndi Eva (4:25);
- Kunalibeko olapa mumatsiko omwe Enoch anayenda ndi Mulungu (5:21-24; Jude 14, 15);
- Kunalibeko olapa mumatsiku a Lameki, munthu yekhayo ozimva pa kupha (Gen. 4:23) munthu odandaula zokhuza Mulungu (5:29);

- Kunalibeko olapa mumatsiku amene Nowah ndi ana ake a amuna anakhulupirira Mulungu ndikukonzeka (5:32).

Anthu anasanduka a upandu ndikumamenyana wina ndi nmzake. Palibe yemwe anali otetezeka. Panalibepo lamulo lironse kapena kotho, choncho Lameki sanalangidwe pamene amazitama pa zakupha.

Chisomo ndi kudekha kwa Mulungu kudikira (1 Peturo 3:20).

Moyo unayamba ndikusamvera ndi kupha ndipo zosatira zake kukhla kuzitamandira makupha. Thupi lamunthu silinali lopatulika ngati mmene Mulungu analamulira kuti zikhali (9:5-6). Mumatsiku amenewa, ambiri amakhulupirira Mulungu koma ochepa ndiwomwe amalapa.



Lankhulani za izi:

1. Ndichisankho chiti ndimene Mulungu anamupasa Kaini (4:4-7)? Chani?
2. Tikuphunzirapo chani pakulemekeza Mulungu kea Kaini (4:3, 5, 9)?
3. Kodi Baibulo likufotokoza motani za fuko la Kaini (4:19-24)?



Ganizirani za izi: kodi Kaini anakwiya ndindani: iye mwini, mchimwene wake kapena Mulungu? Kodi timakhala bwanji mukudziwa kuti yesu anazudzika ndikufera machismo athu ndi ena ndiponso kuti azabweraranso panthawi ina iliyonse?



Mulungu pa ntchito munthawi ya uchimo wawukulu

Kupatula tchimo lawo, Adamu ndi eva anachitira umboni za zambino za Mulungu. Tchimo lawo analipasira kwa mwana wawo oyamba wamamuna, Kaini ndi kwa enanso, koma anakhalabe ndi moyo kuti awone kuwala kwa Mulungu pa ntchito mwa mwana wawo wamamuna wachitatu, Sefi ndi zidzukululu zake.

Enoch anapita kumwamba (5:21-24) ndipo pambuyo pa imfa ya Adamu, Mulungu ana utsa Nowah, chidzukululu chake cha Enoch okhulupirika. Lameki bamboo a Nowah anati, "mwana uyu azatitonthoza ife pamene tikugwira ntchito. Azatitonthoza pamene manja athu azavulala ndikugwira ntchito kwambiri. Pacjifukwa chakuti Ambuye Mulungu wamphavu zonse wayika themberero pa nthzka" (5:29).

Nowah samalabada zamadandaulo a bamboo ake ndipo amangogwira ntchito molimbika, kukhulupirira Mulungu ndi kukhulupirira lonjezo limene linaperekedwa kwa Eva la mpulumutsi (3:15).



Kuwerenga Baibulo: Genesis Mutu 6 ndi 7



Phunzirani za zizi: *Mmene Mulungu anakonzera kuti awonongw dziko lapansi chifukwa cha kufooka kwake (mutu 6:1-7); kukonza kwa Mulungu kuti asiye nowa ndi banja lake ndi moyo pomanga chombo chachikulu asanatumidze chigumula chachikulu (V. 8-22); mmene Mulungu anagwirisira ntchito Nowah ndi banja lake kupulumusa mbalame, zinyama ndi nyerere kugwirisa ntchito chombo mu matsiku zana limodzi ndi mathumi asanu achigumula (Mutu 7:1-24).*

KUCHOKA KU KUKUYIPA KUPITA KUKUYIPITSITSA

Chiyambi cha mutu 6 chimafotokodza mmene zinthu zimayipirayipirabe chifukwa cha zokhumba za munthu pochimwa (6:5-6; 11-12). Mulungu ananyasidwa kuti anapanga muthu pa dziko lapansi. Mtima wake unadzadza ndi ululu (6:6). Mulungu anaconda chilengedwe chake koma dziko lapansi linazaza ndi zofooka zambiri.

Ngakhale sitimvesetsa zinthu zimene zimafotokodzedwa mumalemba akalewa, timaziwa kuti Mulungu anali osasangala chifukwa:

- Mulungu amaona zonse (6:5). Mulungu sakhala kutali kuti sangaone zochimwa zathu.
- Mulungu amazudzika pamene tikuchimwa (6:6). ali ndizomverera. Tchimo limabweretsa kuzudzika ndi imfa kwa anthu amene iye anawalenga ndikuwakonda.
- Patatha dzak zaka, Mulungu anaweluza tchimo ndipo anachitapo kathu (6:7, 13). Amadikira ndikuchitapo kanthu pamene ife ndi am'banja mwathu talephera kulapa.

Mulungu ananganidza zoononga zinthu zamoyo zonse. 'Mulungu anali ndichisoni chifukwa analenga munthu padziko lapanso (6:6). Tchimo limayenera chilango, ngakhalenso imfa.

Chonchobe Mulungu anasintha maganizo ake ndikuganiza zoyambiranso kugwirisa ntchito Nowah ndi banja lake (6:18). Mulungu nthawi zonse amakonzekera zachipulumutso chathu. Chisomo chodabwitsa

NOWAH MUNTHU WACHIKHULUPIRIRO AMANGA CHOMBO CHA MULUNGU

Mulungu wamphamvu zonse anasangalasilidwa ndi Nowah (6:8). Nowah anakhulupirira Mulungu mudziko lomwe linazadza ndi udani ndikuphana. Anali okwatira koma sitikudziwa dzina la mkazi wake. Anali ndi ana a amuna okwatira Shemi, Hamu ndi Yefeti. Anaconda ndi kumvera Mulungu (6:9, 22).

Nowah anali munthu wachikhulupiriro chachikulu ndi wolimba mtima. Anaudza aliyense kuti Mulungu azaweludza dziko lapansi chifukwa cha zofooka zake. Iye anawachenjedza kuti Mulungu aztumidza chigumula chachikulu. Sanafookebe pamene oyandikana nawo amamunyodza iye chifukwa chikhulupiriro chake chinali mwa Mulungu yekha basi (Ahebri 11:7).

Mwachisomo chake ndi chifundo chake Mulungu apulumusa Nowah ndi am'banja lake, anthu asanu ndi mphambu zitatatu. Mulungu anapulumusa nambala yake yochepe ya anthu kuchilango ndi imfa. Timatchula nambala yake yochepeyo kuti "Osalira".

Kenako Mulungu anati kwa Nowah, "ndizathesa anthu onse... choncho zipangire wekha chombo cha matabwa a paini... umu ndimmwnw uchimangire" (6:13-16).



Zombo zinayi za Mulungu zimatchulidwa m'baibulo

- Genesis 6:14. Chombo kapena boti la matabwa a paini kuti liteteze anthu okhulupirira osalira ku chigumula cha Mulungu. Timachitchula chombo cha Nowah.
- Eksodo 2:3. Chombo kapena kuti dengu loluka kuti limuteteze mose amene anazakhala ntsogoleri ndi mpulumutsi wa a Israeli.
- Deuteronomo 10:1. Chombo kapena bokosi la matabwa a mthetha kuti chiteteze Malamulo khumi a Mulungu munjira yopita ku dziko lolonjedzedwa ndi kenakonso munyuma ya Solomoni yopembedzera ku Yerusalemu.

Chombo chilichonse chimagwirisidwa ntchito kupereka chiyambi chatsopano kwa anthu Mulungu. Amali gawo la mapangano a Mulungu ndi munthu.

Chombo chachinayi chinawonesedwa kwa Yohane ndi Yesu khristu mu masomphenya:

- Chivumbuluso 11:19. Chombo cha matabwa chotchedwa bokosi cha chipangano cha Mulungu munyumba ya Mulungu kumwamba.

Mulungu anapanga panga chinngalawa cha Nowah. Mawu oti nngalawa ndi akale kwambiri. Anagwirisigwa ntchinso mu Eksodo 2:3, Detironomo 10:1 ndi Chivumbuluso 11:19.

Chombo chimakhala ndi mulingo wakewake operekedwa ndi Mulungu, pafupifupi mulingo wa mamita zana limodzi ndi makumi asanu kutayimusa mamita makumi atatu ndikuuyimusanso mamita makumi awiri. Muchaka cha 1609 Dutchman Peter Jansen anamanga nngalawa yake ya mulingo wa gawo limozi lamagawo atatu akukulaku. Inali yokhazikika pa madzi ndipo chimanyamula katundu wochuluka kuposa chombo chamulingo omwewu chakale munthawiyo

Mu Genesis 6:17, Mulungu anabwereza za chilinga chake chofuna kuwinnga zamoyo zonse ndi chigumula cha madzi. Kenako anayambisa mawu oti chipangano kwa nthawi yoyamba (06:18. Ili silonjezo ngati lomwe anapanga kwa Adamu ndi Eva. Pangano la Mulungu ndi Nowah, ndi mapangano ena osatirawo anali ofunikira kwambiri pamene nthawi imapita. Onse anali gawo lachipulumutso chomwe amakonza kwa anthu ochimwa. Chipangano choyamba cha Mulungu chimanenedwa pa Genesis 6:18 chinakwaniridwa pa Genesis 8:21 mpka 9:17.

Tsiku litafika kuti Mulungu atumize chigumula kudziko lapansi, anayitana Nowah, "Pita muchinngalawa iwe ndi banja lako" (Gen. 7:1).

Ngati bamboo amayitanila ana ake kuti abwere mnyumba kuthawa mvula ikamabwera. "Lowani! Lowani!" Mulungu ayitana, koma anthu ambiri samvera. Nowah yekha ndi mkazi wake ndi ana ake a amuna atatu ndi azikazi awo a anawo okha ndiwo analowa munngalawayo.

Kenako nyama ndi mbalame zinabwera kwa Nowah. Sanachite kupita kukazisaka. Mulungu anazitumidza. Nowah anatenga nyama zowonjezera kuti apereke nsembe kwa Mulungu ndiponso kugwirisa ntchito ngati chakudya m'malo mwa zamasamba.

Kenako Mulungu anawasekera. Chifukwa chani izi zinali zoyenera? Kuonetsetsa kuti ali wotetezeka, ndikuwasiya ena onse panja. Mpakana p[anthawiyo, nthawi yonse] khomo la chombo linali losekula. Mawu a Mulungu kwa anthu onse lero ndiakuti aliyense olapayo angathe kupulumusidwa kuzera muchikhulupiriro mwa mwana wake, YESU Khristu (Chivumbuluso 22:12-17).

Mulungu anapasa munthu mwayi omaliza wa matsiku asanu ndi awiri kuti avomeredze mwayiwo Genesis 7:4). Alipo yemwe analapa

ndikukalowa mu ngalawayo? Ayi, palibe anabwera chisogolo ndikuza sakanizana ndi Nowah ndi Banja lake. Tsiku lachisanu ndi chiwiri linadusa monga mwa matsiku onse, amuna ndi akazi 'akudyerera, kumwerera ndikukwatirana...' (Luka 17:26-27).

CHIGUMULA CHIBISA DZIKO LONSE

Kenako Mulungu akatseka chiseko cha ngalawa. Tsiku limene Nowah anasekeredwa mungalawa, kunayamba kuvumba mvula. Iyi inali nthawi yoyamba kuti mvula igwe padziko. Komanso madzi ochokera kugawo lakuya la Nyanja anatuluka ndikusefukira kumtunda. Komanso madzi anaphulika kuchoka pansi pa Nyanja (7:11). Posakhalisa dziko lonse zinaphimbidwa ndi madzindipo ngalawa inayamba kuyandama.

Nsonga zamapiri onse zinabisidwa ndi madzi ndipo zamoyo zonse zinafa kupatulapo nsomba. Taziwa mphavu ya mawu awa:

- 'Evary living thing...' (7:21).
- 'Chamoyo chilichonse...' (7:21).
- 'Chilichonse cha panthaka chomwe chimapuma moyo ndikuyenda padziko...' (7:22).
- 'Chinthu chamoyo chilichonse pamaso pa dziko...' (7:23).
- "Nowah yekha ndiyemwe anasala ndi omwe anali naye mungalawa' (7:23).

Nowah sanadziwe komwe anali. Moyo wake unali mmanja mwa Mulungu. Ichi ndichisanzo chabwino cha chikhulupiriro chamunthu. Tikazikhulupira tokha kwa Mulungu, iye amatisamalira ife (1 Peturo 5:7). Kwa matsiku zana limodzi, Nowah



Mulungu anati kwa Nowah, "pita mungalawa ndi banja lako lonse... Tenga nyama zoyela zisanu ndi ziwiri kumthundu uliwonse. Tenga nyama ziwiri kumtundu uliwonse wanyama zomwe sizoyeresedwa. Utenge yayimuna ndi yayikazi zayizo"
Genesis 7:1-2.



Kodi Mulungu anatumiza bwanji chigumula chachikulu, ndi chifuka chani

- Munthawi ya mibado khumi kapena yambiri kuchoka kwa Adamu kufika kwa Nowah, anthu anapanga tekinologe yasopano ndi luso lazipangizo za mkuwa ndi chitsulo (Gen. 4:22) malonda, ulimi ndi nyumba (Luka 17:28) ndinso nyimbo (Gen. 4:21). Koma sanabweretse ulemerero kwa Mulungu: anapanga zochimwa zambiri.
- Anatengeka ndi zosangalatsa, kugonana, kudya ndikumwa (Gen. 6:2; Luka 17:27).
- Amaganiza ndikupanga dongosolo la zinthu zoyipa nthawi zonse (Genesis 6:5).
- Amayankhula mawu olakwika kwa Mulungu, kung'ung'udza, kumpezela zolakwika, kuzikweza okha ndikuyankhula za ena kuti apezerepo mwayi iwowo, kusatira zikhuymbokhumbo zawo zoyipa (Jude 14:15).
- Mtopola unaliponse (Genesis 6:11, 13).
- Mafuko anali okonda katangale kwambiri (Genesis 6:12).
- Sanagwirise ntchito nthawi yowonjedzera yomwe Mulungu anawapasa pamene chingalawa chimamangidwa kuti abwerere kwa Mulungu ndikuti alape (Mateyu 24:38; Ahebri 11:7; 2 Peturo 2:5).

Mulungu analola zaka zambiri ziduse kuti anthu absinthe njira zawo koma sanasinthe (Genesis 6:5). Mulungu anadekha (1 Peturo 3:20). Nowah yekha ndi banja lake ndiwomwe anali okhulupirika munthawi imeneyi. "Nowah anayenda ndi Mulungu" (Gen. 6:9).

anamvera Mulungu pakumangiratu chingalawa kudikirira tsiku la chigumula. Anasunga chikhulupiro mwa Mulungu.

Sopano kwa matsiku zana limodzi ndi makumi asanu, Nowah anakhala akudikirira Mulungu kuti amukumbukire. 'chingalawa chinayandama pamwamba pa madzi' (Genesis 7:18). Nowah samayesera kuwongolera cgingalawacho. Muchifuniro cha Mulungu, nkristu amakwezedwa mwamba pa ziwanda, mmene Atate wathu wakumwamba amatisamalira ife. Tingathe kumukhulupirira kuti akhale olamulira miyoyo yathu.



Lankhulani za izi:

1. Chifukwa chani Mulungu anali ndi chisoni kuti analenga munthu (6:6, 13)?
2. Chinamusiyitsa Mulungu kuwononga anthu onse ndi zinyama ndichani (6:8)? Kondi Osalira ndekuti chani?
3. Ndinani anapangisa zinyama ndi anthu kupita mu chingalawa cha Nowah (7:7-9, 13-16)? Anawatsekera iwo ndi ndani?



Kuwerenga Baibulo: Genesis Mutu 8



Phunzirani za izi: *mmene chingalawa chinakhazikikira panso chitatha chigumula (verses 1-14); Mulungu analamulira Nowah ndi banja lake ndi zinyama zonse kuti zitukule muchombo (v.15-19); Nowah anamanga guwa ndikupereka*

nsembe kwa Mulungu imene iye anayilandira ndikulonjedza kuti sadzatembereranso dziko kachikena (v.20-22).



ANTHU ASANU NDI ATATU APULUMUSIDWA

Sopano madzi ochokera pansi panyanja ndi akumwamba anakumana (8:2). Mulingo wamazizi unachepa (8:3). Pakutha pa matsiku zana limodzi ndi makumi asanu, chombo china khazikika pa mwamba pa phiri la Ararati, ku Ameliya, kummawa kwa turkey. Patapita matsiku makumi anayi Nowah anasekula zenera lapamwamba pa chombo. Anatomiza khwangwala koyamba kenako anatomidza nkhunda.

Ndichifukwa chani Nowah anadikira matsiku makumi anayi? Chifukwa choti amayenda ndi Mulungu. Anali munjira imodzi ndi Mulungu (Amos 3:3). Nowah amafunsa Mulungu choti achite. Iye Sanali ndi phuma. Iye amadikira mayankho a Mulungu ndipo Mulungu anamupasa. Nkhunda inabwerera kwa Nowah ndi samba lantengo wa olive kukamwa kwake. Nowah anadikira matsiku ena asanu ndi awiri (Gen. 8:12), Kenako anatomanso nkhunda kachikena. Munthawi imeneyi siinabwereranso. Kenako Nowah anachosa chotchingira ndipo anawona kuti nthaka inali yowuma.

Mwina ife tikanalumphamo kunngalawa, koma Nowah anadikirabe. Kenako Mulungu anati, "Tuluka munngalawa... Tulusa chinyama chirichonse unalinacho mmenemo" (8:15-17).



Kusintha kwa dziko chitatha chigumula

Dziko lakale chisanafike chigumula linawonongedwa ndi Mulungu (2 Peturo 3:6). Dziko linalinthiratu kwamuyana chifukwa cha machimo a amunthu ndi chilango cha Mulungu kuzera muchigumula. Sopano panali:

- Magawo mazanamazana apansi mumatope olimba munali matupi azinyama zomwe zinafa ndi chigumula; ndiponso magawo okwiririda a zomera kuti apange malasha ndi mafuta;
- Kunalibe magawo amadzi pamwamba kuti atetedze dziko kukutentha kwa masana ndiponso ku kuzizira kwa utsiku;
- Kusintha kwa tsiku ndi tsiku kwa nyengo ndinso mvula ndi namondwe kusatilidwa ndi kuwala kwa dzuwa ndi utawaleza (Gen. 9:14).
- Kusintha kwa nyengo pachaka ndi nthawi yokhazikika yokolola (Genesis 8:22);
- Malo ambiri adziko anasanduka osakhalika mong ngati zipululu ndi malo odzizira;
- kumangika mwachangu komanso kutsogola kwa matalala ndi ayezi;
- nyengo zovuta kukhala zinafika zimene zinapangisa anthu ndi zinyama kuti zisamakhalirese nthawi yayitali ndipo mitundu yazinyama zina sizinakhalenso ndimoyo.

(Gwero: H. Morris, *The Genesis Record*, Baker Books)

NOWAH AMANGA GUWA CHA MULUNGU

Nowah amanga guwa la Mulungu ndukupereka nsembe yopsereza ya nyama yoyera (8:20). Nowah anamanga guwa ngati njira yoprmbedza ndipo Mulungu anayilandira. Mulungu analandira nsembe ya Nowah. Mulungu anaphunzisa kale anthu mmene angayendere ndi chikhulipiro ndi ku pembeza iye. Mawu oti Guwa kutanthauza 'malo operekera nsembe'. Magazi a nyama yoyela yopanda povulala kapena kudwala ali ndi tanthauzo kwa Mulungu. Timadziwa lero kuti ichi chinali chizindikiro nsembe yamagazi oyera ndi chipulumutso mwa Yesu Khristu, wangwiwo, wosachimwa, mwana wa Mulungu.

Mulungu anakhululukira banja la Nowah ndi kuwayeresha chifukwa cha nsembe ya Nowah. Fungo labwino la yansembe yopsereza linalondwerersas Mulungu. Moyo oyera wa Nowah unamukondweresa Iye. M'malo mwa chilango cha uchimo kwaochimwa kapena kufa, Mulungu analandira nsembe ya mwadzi wanyama yoyera. Mwadziwo kunali kutchingira kapena kuti chitetedzo kumachimo a anthu ku kusamvera, kunyozera, kusowa kwachikondi kapena kulakwa. 'Kupulumutsa ndiye kuti kuyanjanana ndi Mulungu' (Nume 28:22)

Nsembe za nyama zinkalandilidwa ndi Mulungu kumachimo a anthu asnafa Mwana wake, Yesu Khristu (1peturo 1:19-21; Aheberi 9:22). Nsembe ya mwadzi wa nyama inali chizindikiro cha kufa kwa Yesu khristu pa mtanda chifukwa cha inu ndi ine (Aroma 5:8). "Mulungu anawonetsa chikondi chake kwaife mu izi: Ngakhale tinali ochimwa, Khristu anatifela" (Aroma; 8). Yesu anali osalakwa: Ife ndiwolakwa ndi tchimo.



Kuwerenga Baibulo: Genesis mutu 9 ndi 10



Phunzirani za izi: *Mulungu anamulola Nowah kudya nyama yopanga Magazi (9:1-7); Utawaleza oyamba ndi chipangano cha Mulungu ndi anthu (v. 8-17); Kuchuluka kwa anthu padziko kunayamba (v. 18-19); Hamu achimwila bambo ake Nowah choncho Nowah anatemberera m'bando wa Hamu ndikudalitsa ana ake ena Yafeti ndi Shemi (v. 20-29). M'bando wa Nowah ndi ana ake a amuna atatu (Mutu 10 ndime 1 mpaka 32).*

CHIYAMBI CHATSOPANO NDI MAPANGANO AMALONJEZO A MULUNGU

Nowah anali nkulu wa dziko lasopano, monga momwe Adamu analili nkulu wa chiyambi cha chilengedwe cha Mulungu. Chinali chiyambi chatsopano. Mulungu anapanga chipangano chatsopano ndi dziko lapansi gen. 9:8-17) ndikumpasa Nowah chizindikiro. Chizindikilocho unali Utawaleza. Nowah anawuwona kutavumba koyamba. Utawaleza umawoneka ngati mulatho kuchoka pansu kupia kumwamba, ndipo unamupangisa Nowah kukumbukira lonjezo la Mulungu: "madzi sazakhanso chigumula chowonongera zamoyo" (9:15). (Chisanachitike chigumula, kunalibeko utawaleza chifukwa kunalibeko mvula).

Chipangano cha Mulungu ndi Nowah ndi chiopangano chimene anapanga ndi zolengedwa zonse zimene zinali mwina mu zaka zikwi zisanu zapitazo. Patatha pafupifupi zaka zikwi ziwiri popanda lamulo lolembedwa. Mulungu anayamba ubale watsopano ndi Nowah ndi m'bando lake. Ubwino wa Mulungu ukuwoneka mu mawu ake, "Malingana ngati dziko likhalapo, kuzakhala nthawi yobzala ndi yokolola, yotentha ndi yozizira, chilimwe ndi chisamu, usana ndi usiku sizisasiya" (8:22).

Chitatha chigumula
Mulungu anapereka chiyambi
chasopano kwa Nowah ndi
dziko lonse:

- chipangano chasopano ndi dziko (8:20-22);
- Malamulo asopano oti azisatidwa kuti alamulire dziko lapansi (9:1-4);
- chenjedzo: chilango chakupha (9:5-7);
- ubale watsopano ndi iye ndinso lonjedzo muchizindikiro cha utalawedzw (9:8-17);
- Mayesero atsopano ndi mauneneri kwa anthu kudzera mwa ana a Nowah (9:18-29).

Muchipanga chaike Mulungu analonjedza, "sindizayikanso

thembere padziko chifukwa Chamunthu. Sindizathembereranso angakhale mtima wake ukulondoleredwa kuzoyipa. Maganizo ake ndiwoyipa kuchokera ali mwana. Sindidzawononganso zinthu zamoyo zonse kachikena, ngati mmene ndachitira. Malingana ngati dziko likhalapo, kudzakhala nthawi yobzala ndi nthawi yosonkhanisa zokolola. Malingana ngati dziko likhalapo, kudzakhala kuzizira ndi kutentha. Kuzakhala chilimwe ndi chisanu, usana ndi usiku" (8:21-22).

ANA A AMUNA ATATU A NOWAH

Ana a amuna a Nowah, Shemi, Hamu, Yafeti, anali ndi mabannja a akulu. Mulungu anawawudza, 'belekani ana ndimuchulukane kuti mudzadze dziko lapansi' (9:1). Posakhalitsa anamwazikana padziko kuti alizaze dziko ndi anthu, kwa iwo ndikumene tichokera (9:19).

Munthawi imeneyi, yetsero lasopano linabwera kwa Nowah. Zimene zinachitika zinasintha mtundu uliwonse waanthu. Asadayambe kumanga nngalawa, Nowah anali mulimi ndinso olalikira. Chitatha chigumula, anabwreranso kuulimi ndi kusamalira ziweto. Analima ndikubzala ma grepusi. Ma grepusi atapsa, anakonza



Mulungu anati, "ndikupanga pangano langa ndiwe ndi ana ako omwe azabadwe iwe utafa. Ndikulipanganso ndi zolengedwa zonse zamoyo zinali ndiwe nchombo... nthawi zina ndikabweretsa mtambo pamwamba pa dziko, utawaleza uzizawoneka mwayiwo. Kenako ndidzakumbukira chipangano changa pakati pa iwe ndi ine..." (9:9-5)



Pangano Lamulungu

Muchipangano chakare, pangano la Mulungu limatchedwa **pangano lakumvera**. (Mulungu analonjedza kudalitsa anthu ngati azimvera iye). Muchipangano chatsopano, pangano latsopano la Mulungu limatchedwa **pangano la chisomo**. (Mulungu analonjedza kupulumutsa anthu omwe amakhulupirira Khristu).

Mapangano a Mulungu ndi anthu ndi gawo lofunikira kwambiri la uthenga wa m'baibulo. "Ndizapanga pangano langa ndiwe", mu Genesis 6:18, ndiloyamba. Mapangano onse amawonetsa chisomo cha chikondi cha Mulungu ndi chifundo kwa anthu ochimwa.

Pangano ndi munthu ndilopotsa lonjedzo la m'gwirizano. Limatsungidwa ndi Mulungu Mwiniwake ndipo siliphwanyidwa! Timati ndilotsimikizika kwamuyaya ndipo silimachosedwa kapena kusinthidwa.

Munthawi ya chipangano chakale, pangano linkatengedwa chachigwi, mwakuti nyama inkaphedwa ngati nsembe ndi chizindikilo chinkayikidwa kuwonetsa kuti Mulungu asungadi lonjedzo lake. Mupangano lamalonjezano a Mulungu ndi Nowah, linakwaniridwa chigumula chitangotha kumene (8:20 to 9:17). Zinyama zimaphedwa ngati nsembe ndipo Mulungu anapereka chizindikiro cha utalaweza (9:13-17).

Zaka zikwi zisanu zapitapo komabe utalaweza umatanthawuzabe chinthu chomwecho: chifundo cha Mulungu chofuna kupulumusa dziko lomwe analilenga ndipo ife tinaliyipisa ndikulikanika kulisamalira. Pali mapangano ambrinso opangidwa ndi Mulungu osonyeza pangano lake lomalidza la chipulumutso kwa anthu mwa Yesu khristu, amene anafera pamtanda kuti akapulumuse dziko kuchilango chomwe timayenera kulandira.

phwando lalikulu ndi banja lake, ndipo Satana anapeza njira yoti amuchititsire manyazi Nowah. Anali ochimwa mukubadwa kwake ndipo anawonetseranso muzochita zake, nggati mmene timapangira.

Nowah analedzera ndi vinyo watsopano ndipo Hamu amaseka thupi lamaliseche la bamboo ake. Yafeti ndi Shemi anafundisa chamanyazi chabambo awowo (9:23). Mulungu anatichenjedza kuti tisamaseke tchimo (iyambo 14:9). Komanso anatilamula kuto, 'lemekedza makolo ako' (Eksodo 20:12).

Chifukwa Hamu sanalemekedze bamboo ake, Nowah ananenera temberero pa ana a Hamu: 'Otembereredwa akhale Canani!' (Mwina Canani anali ndi Hamu choncho anamuchimwiranso Nowah). Panthawi yomweyo Nowah anadalitsa Shemi (9:26).

Yafeti anaphatikizidwa nawo mumadalitso a Shemi ponena mawu oti: 'Mulungu akulitse dziko la Yafeti; Yafeti azakhala mu tenti ya Shemi' (9:27). Mtundu wa Shemi unali la anthu opembedza kwambiri. Yafeti anadalitsidwa atamusatira Shemi mukukhulupirira Yahweh, Mulungu wowona wamoyo yekhayo. Amatenga chikhulupiriro chawo mwa Mulungu ndi Iwo pamene amakulitsa mayiko awo kudziko lapansi.

Mtundu wa Canani anthu ake anali oyipa amene ankakhala kumene kuatchedwa kuti Israeli pano.

Mulungu anamuwonetsera Nowah zomwe zizachitike ndi ana ake atatu a amuna, ndi anthu ndinso mitundu izachokere mwa iwo. Mbiri ya dziko yawonesa kuti ulotsiwo unali wowona.

Nowah anati, 'Odala ndiye Mulungu, Mulungu wa Shemi (9:26). Kodi Nowah anaziwa kuti Shem anali ndi chikhulupiriro kuposa abale aka anja mwa Mulungu wamphavu zonse? Kapena ndilonjezo la Mesiya wa Mulungu kuti azabwera kuzera mu m'bado wa Shemi kuphatikizapo Abrahamu ndi amayi a Yesu Khristu?

Nowah anapempha Mulungu kuti adalitse dziko ndi m'bado wa Yafeti. Kenako anapempha kuti m'bando wa Yafeti ukhale paubale wachinzake ndi m'bado wa Shemi (9:27). Izi ndizoonana mumasiku ano pamene Uraya ndi ku mpoto kwa Amerika akuthandiza A Israeli.

Komabe, Nowah anapempha Mulungu kupanga mibado ya Canani kuzakhala akapolo a mibado ya Shemi ndi Yafeti, zimene ndizoonanso pamene Mulungu



Chiyambi cha chipembedzo pa dziko

Anthu apadziko anachokera kwa ana a amuna a Nowah: Shemi. Yafeti ndi Hamu. Kudzera mwa iwo tingathe kuwona mmene mayiko ndi zipembezo za dziko lapansi zinabwerera. Mawulosi ndi matemberero a Nowah akhazikitsika (9:25-27).

1. Mtundu wa Canani (Mwana wa Hamu) unali oyipa muphnatikizanso ma Amori, ma Havi ndi ma Yebusi. Amapereka nsembe ana ndipoanachita zinthu zoyipa zambiri zimene zinakwiyitsa Mulungu, kuphatikizanso machismo aku Sodomu ndi Gomora. Mulungu anatumiza ana a Israel kukakhala kudziko lawo ndikukawononga kapena kuwalamulira a Canani.
2. Ana ena a Hamu anapita ku Afirika kenako anapanga mtundu wa anthu akale aku mwera kwa India, Ositirelia ndi kumwera kwa Amerika. Anatenga chikhulupiriro cha Mulungu wolenga koma ndikuphatikizanso kulambira mizimu muchipembezo chawo.
3. Mtundu wa Shemi unamwazikana ku Asia komanso kumpoto kwa Amerika. Anatenga chikhulupiriro chawo mwa Mulungu wolenga, kenako anapanga zipembembenzo zina zambiri zineme timazionabe mpaka lero. Anthu okhawo aku Semiti ochokera ku banja loyamba la Abrahamu anasunga chikhulupiriro mwa Mulungu mmodzi wowonayo. Awa anali ana a Yakobo (otchedwa Israeli), zizukulu za abrahamu.
4. Mtundu wa Yafeti unamwazikana ku Uraya, panthawi yovuta amakulitsa ufumu wawo kapena dziko lawo kudzungulira padzikoli. Izi kuphatikizapo maufumu aku Girisi, Roma, Uraya ndi anthu aku Sikandinavi. Pambuyo pake British, Dutch, French, Spanish, Portuguese ndi Belgian anakulitsa maufumu awo padziko lonse lapansi ndipo anatenga chikhulupiriro chawo mwa Yesu Khristu ndiiwo, chimene chinayambisidwa mu zana loyamba ndi zana lachiwiri chiwukireni Yesi.

Kotengedwa: Dave Hisley, *Tishrei Study Paper No. 3.*

anapasa chipambano a Israeli pa a Canani patatha zaka pafupifupi chikwi ndipo zidakali zowona mpakana lero.

Chipulumutso ndichotheka pa zidzukuluzonse za Nowah kuzera mukukhulupirira Yesu Khristu (Lika 24:46-47)

NIMRODI ALAMULIRA OPANDA MULUNGU

Kuchokera ku m'bado wa Hamu, Canani ndi Nimrodi aatchulidwa mwapaderadera m'baibulo. Nimrodi anapanga maufumu ndukumanga midzinda (Gen. 10:8-12). M'dzinda wawukulu oyamba anamanga nimrodi unali Babulo. Kenako, Nimrodi anamanga Ninevah.

Nimrodi anapanga boma limene limalimbana ndi Mulungu, ndipo anayambitsa chipembedzo chasopano chama fano. Iye anali 'mulenje wamkulu'. Munthawi imeneyo mafumu amawonetsa mphavu zawo ndi kuchenjera kwawo pokasaka mikango. Rock Carvings amawonetsa zithunzi za mafumu akusaka mikango.

Nimrodi atamwalira, anthu amamupembeza ngati 'Belusi', kapena Beli. Babelo unali m'dzinda woyamba wa Nimrodi. Nimrodi anasonkhanisa anthu kupita kumizinda ing'ono ing'ono ndipo anamanga makoma kuti awateteze. Mizinda ing'ono ing'ono inasanduka mizinda ikulu ikulu mene imatchedwa mizinda yamumayiko kapena mawufumu (10:10).

Panthawi imeneyi anthu amagwiritsa ntchito:

- njira yoyezera madecimo yomwe imagwiritsidwa ntchito masiku ano;
- sayansi ya masamu;
- dongosolo la cuneiform lolembera kugwirisa ntchito zizindikiro zooneka ngati mphero mu dongo lonyowa ndinso Kenako anawotcha mapalewo padzuwa mpaka atalimba;
- malamulo amene anakopera pa miyala yadongo.



Lankhulani za izi:

1. Chitatha chigumula, ndilonjedzo lanji lomwe Mulungu anapereka (8:20-22; 9:8-17)?
2. Mulungu anawuza chani Nowah ndi banja lake kuti achite (9:1-7)?
3. Kodi Nowah ananena chani kwa ana ake a amuna atatu (9:24-27)?



Kuwerenga Baibulo: Genesis mutu 11



Phunzirani za izi: *Kumangidwa kwa Babulo ndi Nimrodi, imene Mulungu anayitsokoneza (v. 1-9); Mitundu ya Shemih ndi ya terah, bambo ake a Abram (Abrahamu) asanachoke kupita kwa Harani munjira yake yopita ku dziko la Canani (v. 10-32).*

ANTHU AYIWALA MULUNGU

Munthawi ya Nimrodi, "dziko lonse linali ndi chiyankhulo chimodzi..." Mulungu anamulamula Nowah kuti "chulkanani ndimudzaze dziko lapansi" (9:1). Koma anthu ambiri anapita kuchigwa cha Babulo. Ankakhala limodzi kuti atetezeke

komanso kuti azithandizana. Chilankhulo chimodzi chinawathandiza kuti azikhala limozi, kulumikizana bwino ndikumakwanitsa zomwe amafuna kuti apange.

Nkhani yaku Babelo imatiuza mbiri ya chifukwa chimene Mulungu anapangira chiyambi chasopano.

Zaka zambirizinadusa ndipo maganizo achigumula anachoka mwachangu mumaligaliro mwa anthu. Anthu samaganizira za Mulungu (Aroma 1:21-25). Anthu anapeza njira ya tsopano yomangira. Amapanga njerwa za dothi ndikumaziotcha (Gen. 11:2-3). Amagwiritsa phula pomanga njerwazo. Zisanachitike izi, anthu ankakhala muma tenti omangidwa ndi miyara.

Zomwe amamanga zimasungidwa mu ziggurati zimene zimakafika kudzuwa. Zimaoneka ngati ma pilamidi ndimasitepe mbali zonse kupita mmwamba. Pamwambapo panali malo omwe amagwiritsa ntchito kupembezera dzuwa. Babulo anali ziggurat. Ziggurat wina anayimikidwa kukafika mmitambo ku Ur wa Kadesi kumene Abramu (Abrahamu) amakhala.

MULUNGU AWONONGA ZINTHU ZONSE ZA MUNTHU

Anthu anati, “Bwerani tiyeni tizimangire tokha mdzinda. Tiyeni timange nsanja imene ikafike mulengalenga. Tizipangira dzina tokha. Choncho sitizamwazikana padziko lonse lapansi.”

Mulungu anatsika pansu kuzana m’dzinda ndi nsanja zomwe anthu amazimangira. Mulungu anati, “ndi anthu amodzi, ndipo onse aiwo akulankhula chiyankhulo chimodzi. Ndichifukwa chake angapange izi. Sopano angathe kupanga chilichonse chimene angachiganize.”

Yankho la Mulungu linali loti: “tiyeni Ife tipite tikasokonedze chilankhulo chawo...” (Gen. 11:7). Mulungu anatsika kumwamba ndikuzaweludza anthu aku Babulo. Anawa mwaza padziko lonse lapansi ndipo anasiya kumanga m’dzindawo (11:8). (Onani mawu oti ‘Ife’, kuonesera atatu mu Mulungu m’modzi, Atate, Mwana ndi Mzimu woyera. Izi zimatchulidwa kuti Utatu Oyera).

Mulungu sanawononge anthu amenewa ku Babulo, koma anangowasokonedzera chilankhulo chawo. Siku lina anayankhula ngati amodzi ndikugwirantchito molimbikka. Ntchito inkayenda bwino kenako mwadzidzidzi, ndimopanda chenjedzo, omanga sakamumvanso munthu yemwe amagwira ntchito pafupi naye! Ndiponso sakamva zomwe ambiiri mwa anthu enawo ankalandula. Choncho ntchito yayikulu yomanga babulo mwadzidzidzi inayima. Ndichifukwa chake Babulo lero amanthauza ‘chisokonedzo chamawu a phokoso’.

MULUNGU AYITANA ANTHU A CHIKHULUPIRIRO

Mbiri ya m’bado wabanja la Shemi ikuperekedwa kosatiraku. Kuyenda kwamibado kuchokera pa Shemi kuzafika pa Abramu (Abrahamu) kuli ndi mayina khumi (Gen. 11:10-27). Kuchokera ku zimenezi tikhoza kupanga chati cha nthawi chimene chimaonetsa kuti chilengedwe cha Mulungu chakhala kwazaka zochepera zikwi khumi zapitazo ndipo chigumula chinachitika muzaka zochepera zikwi zisanu zapitazo. Akaswiri a sayansi ambili amakhulupirira kuti dziko lapansi ndi mayiko

onse ndi a ang'ono, osati zaka ma miliyoni ngati mmene amaphunzira mumasukulu ambiri.

Muzaka zoyambirira kwakulengedwa kwamunthu, taphunzira kuti anthu ankazipereka kumayetsero a satana ndikumakanika kumvera Mulungu. Sankalapanso pachimo awo ngakhale Mulungu atawawuza iwo.

Tikuziwanso kuti Mulungu sankasiya munthu kuti apitiridze njira zake zochimwa. Ankatumiza chilango komanso amasankha anthu achikhulupiriro ndikupanga nawo pangano. Osalira wokhulupirira weniweni azapitiridza chilungamo chake ndi pangano kupita kutsogoloku ndikukhala mboni yake padziko lapansi.

Timadziwanso kuti kwakhala nyengo zikuluzikulu mumbiri pamene anthu amatembenukiranso kwa Mulungu (4:26).

Nthawi yoyeneraitfika, Mulungu anatumidza mwana wake, Yesu khristu, kuzapulumsa anthu kutchimo. Anabwera kuzayang'ana otayika ndikuwapulumutsa (Luka 19:10). Tsopano, ndichikhulupiriro mwa Yesu, tingathe kubwereranso kwa Mulungu. Ochimwa opulumutsidwa angathe kukalowa kumwamba chifukwa Yesu analangidwa m'malo mwathu. Chiwerudzo cha Mulungu chimafikira kwa iye, choncho timayenda mwaufulu. Yesu khristu anatsekula zitseko zakumwamba kwa anthu onse (Chivumbulutso 22:17). Mulungu anatumidza Yesu kuzatenga chilango chathu cha uchimo.

Mulungu anakonda dziko lomwe analilenga. Koma munthawi yachigumula cha Nowah, analanga anthu chifukwa choipitsa zomwe anazilenga. Anati sazapanganso zimenezo kachikena. Munthawi ya Yesu, analanga mwana wake m'malo molanga anthu chifukwa chzochimwa zawo.

Chikumbutso cha mutu 11 chimatiuza zokhudza m'bado wa Terah amene banja lake linamvera kuyitana kwa Mulungu kuti achoke kwawo. Ikuphatikizapo abramu, yemwe anakhala Abrahamu, amene anayitanidwa ndi Mulungu kuti choke kwawo ndichikhulupiriro kukakhala kudziko lalonjezo lotchedwa Canani, mwana wa Hamu osamvera (11:31). Banja lonse la terah linachoka kupita kwa Harani kumene Terah anakhal ndi Kumwalira.

Nkhani ya zomwe zinanchitikira Abramam ndi mwana wake Isaki ndi mdzukulu wake Loti ndi mutuwa wa Ndemanga za m'baibulo za Manna Publications, Genesis gawo 2. Mulungu anagwiritsa ntchito banja la abramu kukonza njira, m'zaka mazana asanu, kwa anthu opatulika a Mulungu, a Israeli ndi kunyumba kwawo kufupi ndi kuyerusalemu. Izinso zinakonza njira, m'zaka zina chikwi chimozi ndi mazana asanu ndi awiri, yakubadwa kwa Mpulumutsi wa a Israeli, Yesu Khristu, kufupinso ndiyerusalemu.

Anthu lero amasangalala kumanga mizinda ndi misanja chifukwa cha ulemerero wawo. Koma alibe chikondi kapena choonadi cha Mulungu mkati mwawo. Anthu oyera a Mulungu sasaka mumanganso Babulo koma m'malo mwake amasangalala kumanganso Yerusalemu, kukonzekera kubweranso kwa Yesu Khristu padziko lapansi. Choncho, chinthu chofunikira ndi kukonzatso miyoyo yathu kukhala yopanda tchimo kenako kupempherera chitsitsimutso. Izi

zimayambika kudzera muchikhulukiro cha Mulungu ndi revival mwa ife, ndianthu ake.



Mulungu analenga Dziko ndichikondi

Baibulo limatiuza kuti Mulungu analedwa dziko, zinyama ndi anthu pozisangalatsa iwe mwini. Mulungu ndi chikondi (1 Yohane 4:16) ndipo Mulungu anaconda chilichonse ndi ndiamene anamulenga (Gen. 1:10, 25, 31). Zonse zinalibwino pamatso pake, makamaka munthu (Aefeso 2:4). Anatilenga ife kuti tikakhale ndi ubwezi wapaderadera ndi iye, kuti azitithandiza ife ndikutinso tikakhale ndiye kwamuyaya. Ndiponso anatipanga ife ngati iye mwini (muchifanidziro chake) kuti tikathe kukonda anzathu ngati iye. Chikondi chenicheni chimayenera kuperekedwa mwaulere ndi kufunitsitsa mwa chifundo cha Yesu Khristu ndi mumphamvu ya Mzimu Woyera.

Mulungu analenga mamuna ndi mkazi, nyamata ndi ntsikana, kuti amukonde ndikumulambira. Koma satikakamiza kumukonda. Anatipanga ife kuti tizikatha kutsankha kumukonda iye kapena ayi. Mulungu anamulenga munthu moti anthu kuyenda njira zake: ndi Mulungu ndiponso chikondi chake kapenanso opanda chikondichake kapena chaena.

Pamene Adamu ndi Eva anachimwa koyamba, anasankha kuyenda njira zawo. Kuyambira nthawi imeneyo, anthu amafuna kumayenda njira zawo opanda Mulungu. Kutsusana naye Mulungu ndi tchimo. Tonse timayamba Moyo ngati ochima (Aroma 3:10, 23). Baibulo limatiuza za ychimo ndiponso limatiuza kuti Mulungu amatikonda komabe azaweluzo machismo athu. Limaonesa kuyipa kwathu. Komanso limaosetsa mmene ochima angabwerere kwa Mulungu, ndikumukonda, ndikukhala m'njira yake kudzera mukuvomera nsembe ndi ndichipulumutso cha Khristu kwa onse amamukhulupirira iye kuti ndi Mwana wa Mulungu. Baibulo limatiuzanso mmene tingakondere Mulungu komanso kukonda anthu ena m'malo molangoganizira za ife tokha.

Njira Yobwerere kwa Mulungu. Mulungu adaonetsa njira yobwererera kwa iye kuzera muchilango, mukulimbikira, munsembe yamagazi, munsembe ya zakudya ndi ndalama, ndichisanso chachikhulupiriro, ndim'tundu wa Khristu, mumalonjezo ndi mumalamulo. Anawonetsa kufunikira kwa njira yobwererera kuzera mu chenjedzo ndi ukapolo, kuzera mukusiyana naye ndi kuyitana kwake. (Timawerenga zazimenezi mugawo la Baibulo muchipangano chakale.) Koma njira zonsezi sizigwira ntchito bwino chifukwa cha kukula kwa machimo la munthu. Choncho pomaliza, Mulungu anawonetsa njira yobwererera kwa iye kuzera mu nsembe yamagazi a mwana wake okonedwa, Yesu Khristu. Iyi inali njira ya Mulungu kuchokera pachiyambi. Kuzera mukukhulupirira Yesu, ochimwa onse amakhulukidwa sopano ndi Mulungu ndikudziwa chikondi chake. Chikondi chotero ndichikondi choyera cha Mulungu atate wathu ndichifundo cha chikondi cha Yesu Khristu mpulumutsi wathundinso mphavu yachikondi cha Mzimu Woyera wa Mulungu. (Timawerenga zazimenezi mugawo la Baibulo muchipangano chakale.)

Phunzirani zabwiri za zinthu izi mu zolemba za Fred Morris, Manna Publications.



Lankhulani za izi:

1. Ndichifukwa chiyani Mulungu anasokoneza zilankhulo munthawi ya Babulo (11:1-6)?
2. Chosatira chake chinali chani, ndipo ndichifukwa chani ichi chinali cholinga cha Mulungu (11:9)?
3. Ndibanja landani limene Abramamu (Abrahamu) anachokera (11:10, 27)?
4. Mwaphunzirapo chani powerenga mitu khumi ndi umodzi wa Genesis? Chasintha chikhulupiriro chanu kwa Mulungu, cholinga chanu cha moyo, ndikumvetsetsa chomwe chinalakwika mudziko lomwe Mulungu analilengali?
5. Mwakumanapo ndi chisangalalo ndi mtendere omudziwa Yesu ngati mpulumutsi, ndi chipulumutso chanu chifukwa chokhululukiridwa machimo ndi Mulungu?

CHIDULE

Ndemanga za M'baibulo pa Genesis 1-11 zatiphunzitsa ife zokhuza chiyambi cha china chirichonse. Zikunenanso zammene tchimo linayipisira dziko lodabwitsa la Mulungu ndikulifikiza poyenera kuti iye akawononge chinachilichonse ndikuyambiranso kuzera mwa banja la Nowah. Timaona zosatira za tchimo paliponse kutizungulira ife. Koma tingathe kukhululukiridwa machimo athu ndi Mulungu kuzera mukukhulupirira ndi kumvera Yesu. Ndi Mbuye Ndi Mpulumutsi wathu.

Taphunzira zinthu zokhudza chilengedwe chodwabwitsa cha Mulungu, tchimo lathu kuzera mukuyesedwa ndi Satana, ukwati, anthu, zilankhulo, zolinga za Mulungu, chiyambi ndicholinga chamoyo ndi chipulumutso chosatha choperekedwa ndi Mulungu. Gawo lina losatira limatiuza zokhuza Abrahamu, Tate wa Ayuda, kudzera mwa mpulumutsi wa Ayuda, Yesu khristu, analonjezedwa kuzadatsa mitundu yonse ya dziko lapansi. Izi zimachitika pamene anthu alapa machimi awo, kukhulupirira kuti Yesu ndi mwana wa Mulungu ndikuyitana iye m'moyo wawo.

Lofalitsidwa ndi:

Manna Publications (UK)

Typeset ndi:

MissionAssist (UK)

Wofalitsidwa ndi:**Yosindikizidwa ndi:****Mulungu watheketsa kuti mabuku ofotozoa Baibulo a Manna asindikizidwe ndi kufalitsidwa mu:**

Angola, Armenia, Benin, Bulgaria, Burkina Faso, Burundi, Cambodia, Cameroon, Chad, Congo Dem. Rep. (Kinshasa and Katanga), Congo Rep. (Brazzaville), Egypt, Equatorial Guinea, Ethiopia, Ghana, Guatemala, Haiti, India, Ivory Coast, Kenya, Kosovo, Liberia, Malawi, Mali, Mexico, Mongolia, Mozambique, Myanmar, Nepal, Niger, Nigeria, Pakistan, Rwanda, Serbia, Sierra Leone, South Africa, Sudan, Swaziland, Tanzania, Togo, Uganda, Zambia, Zimbabwe

ndipo m'zinenero 43 kuphatikizapo 2 za akhungu

Pitani pa webusayiti yathu pa **www.manna-publications.org.uk** kuti mupeze ndemanga zambiri za Baibulo m'Chingelezi chosavuta, Chifulenchi, Chipwitikizi ndi Chisipanishi. Chonde tumizireni kudzera pa webusayiti yathu kuti mudziwe zilankhulo zina.

Wogwirizana ndi **Avail**, UK adalembetsa zachifundo 1017386

Gulu la makolo la **Manna Publications (USA)**: www.mannapublications.org

ZOYAMBIRA Genesis Gawo 1

Mutu 1 mpakana 11

- Chifukwa chiyani Mulungu analenga dziko
- ‘Mawu’ a Mulungu mu DNA
- Ukwati ndi mabanja

- Momwe uchimo umawonongera moyo
- Momwe Mulungu amalanga uchimo
- Chigumula cha Nowa chinafotokoza

BUKU ili likufotokoza mmene Mulungu analengera dziko lapansi ndi zinthu zina zimene zili mmenemo komanso chifukwa chake. Limaphunzitsa zolinga za Mulungu zimene zili zofunika kwa ife masiku ano. Zimasonyeza mmene Chilichonse chinapangidwira mwangwiro kuyambira pachiyambi. Pambuyo pake idaonongedwa ndi uchimo ndi kusamvera. Izi zinachitika koyamba pamene Adamu ndi Eva anagonja ku chiyeso cha Satana ndi kusamvera Mulungu. Limachenjeza kuti Mulungu amalanga uchimo koma amalondeza chiyembekezo kwa amene amamumvera. Limafotokozanso za Chigumula cha padziko lonse cha m’nthawi ya Nowa. Nowa anakhazikitsa kufunika kwa nsembe ya nyama kufikira m’nthawi ya Yesu Kristu, amene anapereka moyo wake nsembe kaamba ka machimo a onse okhulupirira kuti iye ndi Mwana wa Mulungu. Ndemanga iyi ikutha ndi kuitana kwa Mulungu kwa Abrahamu kuti asamukire ku dziko la malonjezo la Kanani zaka 4,000 zapitazo.

MANNA PUBLICATIONS amasindikiza timabuku tating’ono tofotokoza za Baibulo lolembedwa ndi Fred Morris. Kwa zaka zambiri Fred, ndi mkazi wake Lorna, ankayendayenda padziko lonse akuphunzitsa ndi kulalikira. Mabuku ake ndi osavuta kuwerenga, kumva komanso kumasulira m’zilankhulo zina. Amapereka chiphunzitso choyambirira chogwiritsa ntchito panokha kapena kuphunzira pagulu, kuphatikiza zolemba zina za ophunzira Baibulo, aphunzitsi ndi abusa.

MABUKU ameneŵa adzakuthandizani kumvetsa choonadi chochokera kwa Mulungu Wamphamvuyonse. Iye amalambiridwa ndi mamiliyoni a Ayuda ndi Akristu padziko lonse lapansi. Mabuku amenewa adzakuthandizaninso kuti mulandire chipulumutso ndi moyo wosatha kudzera mwa Mwana wa Mulungu, Yesu Khristu yemwe ndi Mesiya wa Isiraeli. Adzakuthandizani kulankhula za chikhulupiriro chanu mwa Mulungu ndi kupemphera kwa iye. Iwo adzakuthandizani kukutsogolerani ku njira yolakwika m’moyo. Iwo adzakuthandizani kukhala ndi moyo wokondweretsa Mulungu kudzera mu chikondi ndi mphamvu ya Mzimu Wake Woyera. Izi zidalonjezedwa kwa okhulupilira onse pambuyo pa kupachikidwa ndi kuuka kwa akufa kwa Yesu amene amakhulupirira kuti ndi Mwana wa Mulungu.

TIMAPEMPHERA kuti mukhale ndi mtendere watsopano ndi cholinga m’moyo pamene mudalira Mulungu, kuwerenga Baibulo ndi kugwiritsa ntchito ndemangazi. Pamene mukuphunzira choonadi cha m’Chipangano Chakale ndi Chatsopano chochokera kwa Mulungu, ganizirani zimene Yesu anaphunzitsa ndi kuzunzika zaka 2000 zapitazo chifukwa cha chipulumutso chanu ndi zimene akukuitanani kuti munene ndi kuchita lero lino kukonzekera njira ya kubweranso kwake.

Manna Publications

MALANGIZO OPHUNZITSA BAIBULO

“Chinsinsi cha Ufumu wa Mulungu chapatsidwa kwa inu” (Maliko 4:11)